


CHISINDIKIZO CHACHITATU

 Usiku wabwino, amzanga. Tiyeni ife tiyimirire tsopano kamphindi chabe kwa pemphero. Ife tiweramitse mitu yathu.

² Atate athu Akumwamba, pamene ife tikumvera iyo—nyimbo yokongola iyo, ife—ife tiri tikuganizira, Ambuye, za . . . kuti Inu muli pafupi. Ndipo ife tikupemphera kuti Inu mudzatirandire ife usiku uno, Ambuye, monga ana Anu, kukhululukira machimo athu onse ndi zolakwitsa, ndi kutipatsa ife a madalitso Anu, pamene ife tiri anthu osowa.

³ Ndipo mu ora lopambana ili limene ife tsopano tikukhalamo, ndipo ife tikuwona, chaka ndi chaka, kukuchita mdima ndi mdima, kwa dziko. Ndipo Kubwera kwa Ambuye kukuwalira walira, pamene Iye akudziwulula Yekha mu . . . mu Mawu Ake ndi mu mawonetseredwe Ake. Ife tabwera kachiwiri, usiku uno, Ambuye, kudzayesera, za msonkhano uno, ndi kudzakupemphani Inu kuti mutsegule kwa ife, Ambuye, Chisindikizo Chachitatu ichi cha Bukhu ili, kuti icho chikakhoze kudziwika kwa ife, kuti ife tikanadziwa choti tichite ndi momwe tingakhalire moyo, ndi momwe tingakhalire Akhristu abwinoko.

⁴ Ine ndikupemphera, Mulungu, kuti Inu mudzampange aliense amene sali Mkhristu muno, usiku uno, kuzindikira zosowa zawo kwa Inu. Perekani izi. Ndipo ine—ine ndikupemphera, Atate Akumwamba, kuti Mkhristu wobadwa kachiwiri aliyense adzazindikire kuti iye ayenera kukhala moyo mofupikira kuposa momwe iye wakhalira mmbuyo, kuti ife tikakhoze tonse kukhala mu umodzi uwo wa chikondi Chachikhristu ndi chikhulupiriro.

⁵ Perekani kuti munthu wodwala aliyense pakati pathu adzachiritsidwe usiku uno, Ambuye. Iwo akuzindikira chosowa chawo cha Inu. Ndipo ine ndikupemphera, Atate, kuti Inu mudzadalitse chirichonse chimene chachitidwa kapena kulankhulidwa, kwa ulemu Wanu ndi ulemerero, mu Dzina la Yesu ife tikupempha izi. Amenii.

⁶ Chabwino, kachiwiri, usiku uno, ife tasonkhana palimodzi kachiwiri kwa ichi, u—usiku wa Lachitatu wa sabata. Ndipo ife tikudalira Ambuye, usiku uno, kwa—kutsanulira kwakukulu kwa madalitso Ake pa Mawu Ake. Ndipo lero ine ndakhala ndikuwerenga, mwa nthawizonse, ndi kuyesera kuganizira za zinthu zomwe zidzakhale zofunikira kwambiri kuzilankhula, ndi chinthu, momwe ndingachilankhulire icho, ndiyeno ndikudalira pa Ambuye kuti apereke kwa ine kumasulira ndi matanthawuzo a—a Mawu awa amene alembedwa. Ndipo ine

ndiri wothokhoza kwa Iye pa zomwe Iye watichitira ife kupyola sabatayi, imene ife . . . ya kutsegula kwa Zisindikizo izi.

7 Ndipo, tsopano, mwina icho chikanakhala chinthu chabwino ngati Lamlungu mmawa, ku. . . Inu mukudziwa, nthawi zambiri. . . Ife sitimatanthawuza kuti tikhale osamvetsedwa, koma, inu mukudziwa, iwe. . . Izo zimafika njira imeneyo. Ndipo kotero, mwina, Lamlungu mmawa, ngati onse amene ali nalo funso mu malingaliro mwawo lokhudza izi, akanadzalilemba ilo ndikulipereka ilo pa tebulo apa, Loweruka usiku, ndipo kotero ine ndikhoza kuwona chomwe ilo liri. Ndiyeno ine ndiyesa kukuyankhirani ilo inu, Lamlungu mmawa, Ambuye akalola. Ine ndikuganiza icho chikanakhala chabwinoko kuposa chimene ife timakonzekera, chifukwa nthawizina sizimamvetsedwa, inu mukudziwa. Ndipo kotero mwanjira iyo ine ndidzapeza— Icho chikanadzakhala chabwinoko kuti ine ndikanadza—ine ndikanadzachitenga icho mowongoka, inu mukudziwa. Icho chikanadzakhala basi chomwe chiyenera kukhala. Chifukwa, nthawizina, tsopano. . .

8 Wina anayitana lero ndipo anati, kuti—kuti, anayitana ndipo amafuna kudziwa ngati izo zinali zowona, kuti, “Pamene m—Mkwatulo udzakhala utachitika, padzangokhala mmodzi mu Jeffersonville ndi mmodzi mu New York, ndipo ena onsewo kutsidya kwa nyanja.” Kotero, onani, icho sichinamvetsedwe basi. Ndiye wina anati, kuti, “Loweruka usiku, ngati Ambuye apereka kwa ife Chisindikizo chotsiriza, ndiye Yesu adzakhala pano Lamlungu mmawa.” Mwawona? Kotero ndicho—ndicho. . . Inu mukuwona, inu—inu musati. . . Izo, izo siziri choncho. Ndipo inu musati. . . Izo siziri.

9 Ife sitikudziwa. Ngati aliyense akuwuzani inu kuti iwo akudziwa pamene Iye akubwera, inu mudziwe kuti iwo akulakwitsa, kuyamba nkuyamba, chifukwa palibe mmodzi amene amadziwa izo. Koma ife tikufuna kukhala moyo, lero, ngati kuti inali pakali pano.

10 Ine ndikhala ngati ndakuzungulitsani inu kwa miniti, kotero khalani okonzeka. Ine—ine ndikukhulupirira Yesu abwera mkati mwa, asanakwane, maminiti atatu kuchokera pakali pano, a nthawi Yake. Inu mukudziwa kutalika kwake iyo ikanakhalira? Pafupi zaka makumi atatu ndi zisanu. Mukuwona, zaka chikwi ziri chabe tsiku limodzi, ndi Iye, inu mukuwona.

11 Kotero, pamene inu mumva mtumwi kumbuyo kuno akuti, “Nthawi ili pafupi,” cha apa, “nthawi ili pafupi.” Mtumwi ananena zimenezo mu Zivumbulutso. Inu mukudziwa kutalika kwake momwe izo zakhalira? Iyo siyinati. . . Limenelo linali chabe dzulo, kwa Mulungu, osati nkomwe masiku awiri.

12 Ndipo, onani, ngati ali maminiti atatu, osakwanira maminiti atatu a Kudza Kwake, onani, zimenezo zikanadzakhala zaka makumi atatu, pafupifupi, kwa ife, kapena chinachake mwa

dongosolo limenelo. Ndipo penyani momwe, chomwe maminiti atatu chikanakhala kwa Iye: Iye ali kale kudzuka, kuti azibwera. Kotero ife, inu . . . nthawizina pamene inu muwerenga apa, Iye akulankhula manenedwe a Mawu, onani, osati mwa manenedwe athu.

¹³ Ndiyeno ngati ine ndikanadziwa kuti Iye anali kubwera mawa usiku, mawa usiku, mawa ine ndikanawerenga ndi kumufunsa Iye kuti andipatse ine Uthenga wa Chisindikizo Chachinai. Ndipo ndikanabwera kuno ndi kudzalalikira Icho, momwemo basi. Mukuwona? Ine—ine ndikufuna kumachita tsiku lililonse chokhacho chomwe ndikamachita ngati Iye akubwera. Ndipo ine sindikudziwa malo ena abwino kuposa kugwidwa pa malo antchito pomwe, mukuwona, pa malo antchito. Kotero ife tizingopitirira mpaka Iye atabwera.

¹⁴ Nthawizina pamene ife tiwerenga kokha, ndipo, tsopano, khalani osamalitsa kwenikweni. Ndipo pamene inu muwerenga, katengeni matepi, kamvetsereni kwa iwo mwatcheru kwenikweni. Chifukwa, inu mudzazipeza izo pa tepi, chifukwa iwo akhala akuseweranso matepi amenewo, ndipo iwo ali abwino kwenikweni ndi omveka. Kotero, inu mudzazimva izo momveka mmenemo.

¹⁵ Tsopano, aliyense mu chikondi naye Khristu, ine ndikuyembekeza, usiku uno, ndipo aliyense akumukonda Iye.

¹⁶ Ine ndikuwuzani inu chimene, nthawizina, chimene chimawasokoneza anthu, winawake uja amene abweramo ndipo sanamvere gawo loyamba la msonkhano, inu mukuwona. Ndiye iwo amabweramo ndipo iwo amakumva iwe ukufanzira mmbuyo, kugunda mmbuyo, chinachake, ndiyeno iwo amatizira chimenecho, chimene chalankhulidwa, ndipo iwo sanamve gawo loyamba. Ndiye zonse ziri zosokonezeka kwa iwo, inu mukuwona, ndiye. Ndipo iwo amaganiza kuti chinachake chinanedwa mosiyana, koma Icho—koma Icho sichiri.

¹⁷ Kotero ngati inu muli nalo funso limene inu simukulimvetsa, ingolembani ilo pa chidutswa cha pepala. Muliyike ilo muno, nthawi iliyonse pakati pa tsopano ndi Loweruka usiku. Ndipo ine ndidzayesa, Lamlungu mmawa, ku . . . Ngati liri lozunguza pang'ono, inu muti, “Chabwino, ine ndikungodabwa chimene *ichi* chimatanthawuza apa. Ine sindinachimvetse icho.” Inu mukudziwa chimene ine ndikutanthawuza. Ndiye ine ndidzayesa kukuyankhirani chimenecho inu, Lamlungu mmawa, Ambuye akalola.

¹⁸ Tsopano, usiku uno ife tiwerenga kuchokera mu Mawu akale odalitsidwa awa kachiwiri, mu mutu wa 6. Ndipo ife tiyambira usiku uno ndi Chisindikizo Chachitatu. Ndipo imeneyo ndi ndime ya 5, ndime ya 5 ndi 6.

19 Ndipo mawa usiku ife titsekera okwera anayiwo; kavalo woyera, ndi kavalo wofiira, kavalo wakuda, ndi kavalo wotumbululuka.

20 Ndipo ine ndikufuna kunena ichi. Kuti, nthawi iliyonse, ngakhale mpaka mmawa uno, pafupifupi. . . Ine ndinadzuka kwenikweni, moyambirira kwambiri ndi kupita ku pemphero zinthu zisanagwedezeke, ndi kumangopitirira kupempherabe kupyola mu tsiku. Koma mmawa uno, molawirira, Mzimu Woyera unabwera kumene ine ndinali. Ndipo momveka basi monga chirichonse, ine—ine ndinawona Chisindikizo china ichi chikutseguka tsopano, chimodzimidzi basi. Tsopano—tsopano—tsopano, Iye akundimva ine, ine ndikudziwa. Ndipo ndiri wothokoza kwambiri.

21 Tsopano, inu mudzangokumbukira kuti pali chinachake chikuchitika. Chimene, ine—ine ndikuyembekeza inu mukuchigwira icho, onani, onani, kuti pali chinachake chomwe chikuchitika. Ine ndikungofuna kuwuyesa mpingo uwu nthawi imodzi, ndi kuwona ngati iwo angakhoze kwenikweni kugwira chinachake icho chisanachitike kumene. Tsopano kumbukirani, kumbukirani zomwe ine ndakuwuzani inu. Ndipo, tsopano, Ambuye atithandize ife.

22 Tsopano mu ndime ya 5.

Ndipo pamene iye anali atatsegula chisindikizo chachitatu, ine ndinamva chamoyo chachitatu chikuti, Bwera . . . udzawone. Ndipo ine ndinapenya, ndipo tawonani kavalo wakuda; ndipo iye amene anakhala pa iye anali nawo miyeso mu dzanja lake.

Ndipo ine ndinamva liwu mkati mwa zamoyo zinai likuti, Miyeso wa tirigu wogula rupiya, ndi miyeso itatu ya barele yogula rupiya; koma ona kuti iwe usawononge mafuta ndi . . . vinyo.

23 Tsopano tiyeni tiyike maziko ichi pang'ono chabe, ndipo pa Zisindikizo zimene ife tazipyola. Chifukwa, monga ngati mu mibadwo ya mpingo, chifukwa, ife timayesa kupereka maziko, kukhala ngati kuchilumikizitsa icho, mpaka inu mukhoza. . . Ndi momwe mibadwo iliri makamaka mu Lemba, umodzi ukulowererana pamwamba pa umzake, kukhala ngati choncho. Monga kukwera makwerero, ndi kukwera sitepe, kani; imodzi kumatsikira pansu kwa imzake, ndi kumabwera mmbuyo chotero, pamene iwe ukupita mmwamba pa sitepe.

24 Ndipo tsopano, Zisindikizo izi, n. . . Ndizo b—Bukhu la Chiwombolo, losindikizidwa. Aliyense akumvetsa zimenezo? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Ndipo Bukhu ili liri losindikizidwa nazo Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri. Ilo liri Bukhu losindikizidwa pasanu ndi pawiri. Mwawona?

25 Ndipo tsopano kumbukirani, monga ife tinawonetsera izo kwa inu, ndipo tinazitenga izo kuchokera ku Yeremiya

ndi onse. Tsopano, iwo, pamene iwo anali. . . Iwo ankalemba monga *chonchi*, pa chidutswa cha—cha cholembapo, kapena pepala, kani; kapena, osati pepala, koma icho chinali chikopa. [M'bale Branham akuwonetsera kukulunga ndi kusindikiza kwa sikololo, pogwiritsa ntchito zidutswa za pepala.] Ndipo iwo ankachikulunga icho, monga *chonchi*. Tsopano icho. . . Ndiyeno kotsirizira kwa icho kunkangosiyidwa monga *choncho*; icho chikusonyeza chimene chiri mmenemo. Ndiye chimodzi chotsatiracho chikudzatenga malo a mtundu womwewo, kukulunga mwanjira yomweyo, kukulunga monga *choncho*. Ndiyeno, pamapeto apa, icho chinkang'ambidwa monga *choncho*, ndi kusiya chimodzi china.

²⁶ Chabwino, limenelo linali Bukhu losindikizidwa pasanu ndi pawiri. Tsopano ife tinalibe konse Mabuku monga ili mpaka posachedwapa. Mabuku mu nthawi yakale anali masikololo. Iwo anakulungidwa. Ndiyeno pamene iwo afuna phunziro kapena chirichonse. . . Monga ngati—ngati Baibulo lakulungidwa, inu mukanatembenuza Bukhu la Yesaya; inu mukanadzakhoza kutsegula mmusi apa ku Yesaya, ndiye nkulifunzulula Ilo monga *choncho*, ndi kuwerenga Ilo. Ndipo ili liri Bukhu losindikizidwa pasanu ndi pawiri la Chiwombolo.

²⁷ Ndipo tsopano ife tikupeza kuti Mwanawankhosa akutulukira, akutenga Bukhu kuchokera m'dzanja la Iye amene anakhala pa Mpandowachifumu, ndipo akumatula Zisindikizo, ndi—ndi kumasula. . . ndi kumasula Izo, kumasula Zisindikizo kwa anthu.

²⁸ Ndipo Zamoyo zinai zikukhala pamenepo, zomwe ife tinazitenga mu mibadwo ya mpingo, Zamoyo zinai zomwezo, inu mukuziwona izo njira yonse kupyola mu Lemba, ndipo izo ziri Izo Zomwe zikuchita kulengeza kwa Zisindikizo izi pamene zikumatulidwa. Tsopano, ndipo ife tikuliwona ilo liri b—Bukhu la Chiwombolo.

²⁹ Ndiye ife tinabwerera mmbuyo ndi kukatenga w—Wowombola Wachibale, ndipo ife tinamutenga Iye, kuti tiwone yomwe inali ntchito Yake. Ndipo tsopano kwa zaka zonse izi, Khristu wakhala akuchita ntchito ya Wowombola Wachibale. Tsopano, onse amene akumvetsa zimenezo, anene, “Ameni.” [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Iye wakhala ali kuchita ntchito ya Wowombola Wachibale.

³⁰ Koma padzabwera nthawi imene pamene ntchito yowombola idzakhala itatha. Ndipo pamene ntchito yowombola yatha, ndiye Iye akusiya Mpandowachifumu wa Mulungu, pamene Iye wakhala tsopano. Koma umenewo suli Mpandowachifumu Wake. “Iye amene agonjetsa adzakhala nane Ine mu Mpandowachifumu Wanga, monga Ine ndalakika ndipo ndakhala pa Mpandowachifumu wa Atate Anga.” Umenewo suli Mpandowachifumu Wake. Umenewo ndi wa Mzimu, Mulungu.

Khristu, Mwanawankhosa, iwo suli wa Iye. Iye ali Mulungu mu thupi, mukuwona; amene ali Mulungu yemweyo, kupangidwa mu thupi. Tsopano, Iye akudzuka kuchokera ku mpando . . .

³¹ Choyamba, kulengeza kunapita apo, pakuti, kwa, “Ndani angakhoze kubwera ndi ku-. . .ndi kutenga Bukhu la Chiwombolo ili?” Mukuwona, pakuti dongosolo lonse la chiwombolo, kuchokera kwa Adamu, zonse zimene Adamu anataya.

³² Kunalibe kanthu kotayidwa mpaka Adamu. Ndipo pambuyo pa Adamu, zonse zinali zitatayika, mu dziko lapansi. Ndipo chirichonse pa chirengedwe cha dziko lapansi chinali chitatayika. Ndipo chirichonse chinagwa naye Adamu, chinawoloka phompho, mwakuti palibe mmodzi akanakhoza kubwerera, panalibe njira konse. Munthu, pamene iye anachimwa, iye anasiya njira yake, iye sanasiye njira yobwererera kwa iyemwini. Ndiyeno a . . .

³³ Pamene funso ili linafunsidwa; Yohane mvumbulutsi, uja . . . mneneri Yohane, anali mu masomphenya ndipo anawona izo. Ndipo panalibe munthu Kumwamba, panalibe munthu pa dziko lapansi, panalibe munthu pansu pa dziko lapansi, kapena aliyense, anali ngakhale woyenera kuyang’ana pa Bukhu. Mwawona? Tsopano ingoganizani za chimenecho! Ndiye Mwanawankhosa akubwera patsogolo, ndipo Iye akutenga Bukhu. Tsopano Yohane anafunsidwa kuti asati alire mopitirira. Iye anati, “Tawona, Mkango wa Yuda walakika, ndipo—ndipo Iye akhoza kutenga Bukhu ndi kulitsegula Ilo.” Kotero, Iye anachewuka kuti ayang’ane Mkango, ndipo iye anawona Mwanawankhosa. Mkulu anawutcha, anati, “Mkango walakika.” Koma pamene iye anabwera ndi kuyang’ana, iwo unali Mwanawankhosa akubwera kuchokera ku Mpandowachifumu.

³⁴ Tsopano, iye anali asanazindikire konse Icho poyamba. Chifukwa? Iye anali ali kumbuyo uko, mu kuchita Kwake kwa ntchito ya ukhalapakati Wake; pakuti Iye anali kukhetsera anthu, kuwatetezera anthu, mpaka moyo wotsiriza, umene unayikidwa pa Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa maziko adziko asanakhale, kubwera mkati. Kudzangokhala ambiri a iwo kumeneko, ndipo ndicho icho. Ndizo zonse. Enawo sadzafuna nkomwe kuti abwere mkati; iwo alibe chikhumbo choti abwere mkati. Ndipo kotero, ndiye, pamene moyo wotsiriza uwo ubwera mkati, ndiye nthawi ya chiwombolo yatha.

³⁵ Ndiye Mwanawankhosa akutulukira kudzatenga ufulu Wake kwa zomwe Iye waziwombola, ndipo ndicho chirengedwe chonse. Dziko lapansi ndi chirichonse ziri za Iye. Mwawona? Iye waliwombola ilo ndi Magazi Ake Omwe. Ndipo pamene Iye abwera apo kuti atenge Bukhu ili, kuti alitsegule Ilo, bwanji, mai, iwo anali . . . Yohane sanalirensa. Ndipo iye anayang’ana,

ndipo Mwanawankhosa uyu anali Mwanawankhosa wophedwa. Iye anali ataphedwa kale, koma iye anali wamoyo kachiwiri. Ndipo tsopano ife tinapeza kuti mwanawankhosa wophedwa ali mwanawankhosa wamagazi, akuwukha paliponse. Iye waphedwa. Atatha Iye kuphedwa, Iye anali atawuka kachiwiri. Iye anali kukhala pa Mpandowachifumu, titi, mmbuyomo kuseri kwa Mpandowachifumu, monga *chonchi*, kutetezera miyoyo yonse iyo imene ikanadzabwera. Ndiye pamene mmodzi wotsiriza anali apa, ndipo iyo inatsirizika, m...Mulungu anagwirizirabe Bukhu la Chiwombolo. Mwawona? Tsopano Iye akungochita ntchito ya Wowombola tsopano.

³⁶ Monga, Boazi anapita kumusi, ndipo Rute anali atangokhala pamenepo kuyembekezera mpaka Boazi...ine ndikutanthawuza, Boazi atachita ku...wachibale, ntchito yowombola. Mukukumbukira ine ndikulalikira zimenezo, osati kale lapitalo? Rute, akukunkha; ndipo, Rute, chirichonse chimene iye anachita; ndipo mpaka mmusi, ndipo chinthu chotsiriza chinali, Rute, kuyembekezera. Mukukumbukira momwe ine ndinazifanizitsira izo mu Mpingo? Pamene, Boazi akupita kumusi kukachita ntchito ya wachibale wowombola. Iye anayichita iyo; anavula nsapato yake ndipo anapanga umboni, ndipo anamuwombola Naomi, ndipo, kupyolera apo, anamutenga—anamutenga Rute. Tsopano, kotero, Rute anali kungoyembekezera, chifukwa iye anali kale atagwirira ntchito. Iye anali atachita zinthu zina zonse izi, koma iye anali kuyembekezera tsopano. Ndiyeno pamene...Mpingo uli kuyembekezera, kupumula (ambiri a iwo, ochuluka a iwo, mu fumbi la dziko lapansi), pamene Iye akuchita ntchito Yake ya Wachibale Wowombola.

³⁷ Tsopano dziko likupitabe chiyipire. Ndipo tchimo likuwunjikika, ndi—ndi matenda, ndi vuto, ndi imfa, ndi chisoni. Amuna opanda umulungu ndi akazi opanda umulungu akufa mmusi momwe. Khansara ikuwadya iwo, ndi china chirichonse, pamene iwo sangakhoze kusunga chikhulupiriro chokwanira kufikira kumeneko ndi kukazigwira izo.

³⁸ Tsopano zindikirani. Koma ndiye zitatha izo zonse, kutatha kukhala Kwake...Kutetezera Kwake kutachitika, Iye akutulukira, akutenga Bukhu kuchokera m'dzanja la Iye. Ndiyeno Yohane, ndi chirichonse Kumwamba, ndi kuyamba... Miyoyo pansu pa guwa ikuyamba kufuwula. Ife tizipeza zimenezo mu Chisindikizo cha Chisanu ndi chimodzi, aponso. Ndipo momwe iwo anasangalalira! Ndipo—ndipo iwo anagwa pansu, akulu, ndipo anatsanulira mapemphero a oyera. Ndipo miyoyo pansu pa guwa inafuula, “Woyenera muli Inu, chifukwa Inu mwatiwombolera ife kwa Mulungu! Ndipo ife tikubwerera ku dziko lapansi, kukakhala moyo monga mafumu ndi ansembe.” O, apo panali chachikulu... .

39 Ndipo Yohane anati, “Aliyense Kumwamba, chirichonse pansi pa dziko lapansi, ndi chirichonse,” chinamumva iye akulemekeza Mulungu pa icho. Yohane ayenera kuti analipeza dzina lake Pamenepo, inu mukudziwa. Nthawi yonse iyo!

40 Ndiye iye anati, “Iye ali woyenera kutenga Bukhu la Chiwombolo.” Tsopano ilo siliri la Woweruza apanso konse. Ilo liri la kwa Wowombola, ndipo Iye wachita ntchito ya chiwombolo.

41 Tsopano Iye akupita kukawuwonetsa Mpingo chimene Iye wachita. Amen. Mwawona? Ndiye Iye akungotenga. . . Koma Bukhu liri lotsekedwa. Palibe mmodzi ankadziwa, konse. Iwo ankadziwa kuti Ilo linali Bukhu la Chiwombolo, pa Ilo apo, koma Ilo liri lakuti liwululidwe mu masiku otsiriza. Malingana ndi Chivumbulutso 10, mngelo wachisanu ndi chiwiri apatsidwa Uthenga wa Ilo. Chifukwa, Ilo linati, kuti, “Mu nthawi ya kuwomba kwa m’badwo wa mpingo wachisanu ndi chiwiri, mngelo wachisanu ndi chiwiri, pamene iye akuwomba, zinsinsi zonse za Mulungu ziyenera kutsirizidwa, mwa kuwomba kwake.” Ndiye, litatha Ilo kuwululidwa, Mngelo akutsika pansi kuchokera Kumwamba, amene anali Khristu. Tsopano kumbukirani, mngelo uyu ali pa dziko lapansi, mtumiki.

42 Pansi akubwera Khristu, inu mukumuwona Iye mu mutu wa 10 wa Chivumbulutso; akuyika phazi limodzi pa mtunda, limodzi linalo pa nyanja; utawaleza pa mutu Pake, maso ngati. . . ndi mapazi ngati moto, ndi zina zotero; akukweza dzanja Lake mmwamba, ndi kulumbira pa Iye amene akhala moyo kwa nthawi za nthawi zonse, pa Mpandowachifumu, kuti, “Nthawi siyidzakhala ponso.” Ndipo pamene Iye akutenga lumbiro ili, Mabingu Asanu ndi awiri akulankhula maliwu awo.

43 Ndipo wolemba, amene, pamene Yohane anatengedwera mmwamba, ankayenera kulemba zomwe iye anapenya. Iye anayamba kulemba. Iye anati, “Usati ulembe Izo.” Chifukwa. . . “Usati ulembe Izo.” Izo ziri zo- . . . Iye anati, “Sindikiza Izo.” Mu chiyani? “Sindikiza. Usati unene Izo.” Mukuwona, Izo ziri zoti ziwululidwe, koma Izo sizinalembedwe ngakhale mu Mawu.

44 Ndiyeno pamene Iye anayamba kutsegula Zisindikizo, ife tikupeza, izo zonse zinali zododometsa. Mwawona? Pamene Iye anategula Chisindikizo Choyamba, iye anaganiza, “Tsopano apa Icho chilankhula, ‘Ndipo icho chidzabwera kuti *chakuti-ndi-chakuti* chidzatenga mpandowachifumu, ndipo *china* kuchita *ichi*, ndipo *ichi* chidzachita *icho*.’”

45 Koma pamene icho chinali, apa iye wapita, kavalo woyera, akukwera, ndipo wokwera ali pa iye. Chabwino, “Iye anali nawo uta mu dzanja lake; ndipo iye anapatsidwa korona, patapita kanthawi,” iye anati. Ndizo zonse.

46 Ndipo Mwanawankhosa anatembenukira mmbuyo kachiwiri, ndipo anasolola Chisindikizo china, ndipo apa panatulukira wakuda. . . wokwera pakavalo wofiira. “Ndipo iye anali nalo. . . anapatsidwa l—lupanga; ndipo iye anali kupita kukapanga nkondo; ndipo anapatsidwa mphamvu yayikulu, ndi kuchotsa mtendere pa dziko lapansi, ndi kuphana wina ndi mzake.” Ichu chinali ngati. . . chinthu chachinsinsibe (sichinali icho?), pamene Iye anachitsegula Ichu.

47 Ndiyeno akupitirira, ndipo anati, “Mu tsiku asanachitike kumene Mbingu Asanu ndi awiri awa, zinsinsi zonse apa zawululidwa.”

48 Tsopano penyani. Ndiye ife tikupeza, monga ife takhala tikuwereka, kuti, kutsika kupyola mmibadwo, ife takhala nawo okonzanso, osati aneneri, Okonzanso! Ndipo udindo uliwonse umatenga yake yake—ntchito yakeyake.

49 Monga ngati munthu amene ali—wosamalira telefoni, iye sali chimodzimidzi wokonza magetsi. Iye akhoza kuchita kantchito pang’ono pa iwo. Ndipo monga, ngati munthu ali munthu wanthambo, chabwino, iye zedi. . . Munthu ali wokumba dzenje la mzati, ndipo sanachitepo konse ntchito iliyonse ya nthambo, iye kulibwino akhale kutali ndi nthambo; koma iye akhoza kuchita ntchito pang’ono yosamalira kapena chinachake.

50 Koma pamene Chinthu chenicheni chiri choti chiwululidwe pa tsiku lotsiriza, la gawo lotsiriza la Mpingo, pali pamene Mulungu wanena kuti Iye alitumiza kwa ife, malingana ndi Malemba. Ndipo ife tachifufuza icho mopyola ndi kupyola, kuti Iye ananeneratu kuti Mzimu wa Eliya ukanabwerera mwa munthu wina. Tsopano, ine ndikuganiza izo zapangidwa momveka basi. Ndipo ife. . . Ndipo ife tikuyang’anira kuti icho chichitike; penapake, munthu wodzozedwa, mu masiku otsiriza, kuti awuke. Tsopano inu mudzamva zambiri za otentheka ndi zina zirizonse, koma izo basi—zikuyesa basi ku. . . Ndiye Mdierekezi, kuyesera kuchotsa kwa weniweniyo pamene iye afika apa, mukuwona. Koma izo zidzazindikiridwa moyenera. Inu mukudziwa chimene Eliya anali; ndipo yang’anani icho, ndipo inu—inu mudzadziwa. Ndiyeno pamene iye. . . Tsopano, Osankhidwa adzadziwa.

51 Osati enawo; iwo ndithudi sadzachita izo. Iwo adzachiphonya Ichu, milioni mailosi. Monga. . . Ife takhala tikupyola zonse izo, ndipo tawonetsa momwe iwo anamuphonyera Yohane, momwe iwo anamuphonyera Eliya, momwe iwo anamuphonyera Yesu, momwe iwo anawaphonyera iwo njira yonse motsatira. Ndipo iwo adzachita chinthu chomwecho, chifukwa Baibulo linati iwo adzatero. Mwawona? Koteri ndiye, mu nthawi imeneyo, Ichu chidzakhala chodzichepetsa kwambiri. Ichu chidzakhala chophweka kwambiri. Ichu chidza. . . chimene chidzawapange anthu kugwa

kuchoka kwa Icho. Ndi chophweka kwambiri kwa iwo. Ife tikupeza, ndipo nthawizonse, pamene anthu akhala anzeru ndi ophunzira, ndi kudziwa zambiri zonse, ndiye iwo basi. . . Ndiwo basi mtundu umene umaphonya izo, inu mukudziwa. Mwawona?

⁵² Yesu sanawatenge anthu oterowo kuti (akhale) ophunzira Ake. Iye anatenga anthu osaphunzira, asodzi, ndipo palibe amene anali wolumikizidwa ndi mipingo yawo ndi zinthu. Iye anatenga anthu wamba chabe, osonkhetsa msonkho, ndi alimi, ndi asodzi, ndi ena otero, kuti agwire ntchito Yake. Mwawona? Chifukwa, iwo—iwo amadziwa kuti sali kanthu, ndiye Iye akhoza kupanga chinachake kuchokera mwa iwo, mwawona. Malingana ngati iwo azipitirira kuzindikira kuti iwo sali kanthu, ndiye Mulungu akhoza kugwira ntchito.

⁵³ Koma pamene iwo afika poganiza kuti iwo akudziwa chinachake, ndiye, “Iwe sikudziwa kanthu kamene iwe uyenera kukadziwa,” Baibulo limatero. Ndipo kotero, ndiye, ife—ife timapeza izo.

⁵⁴ Ndipo tsopano, ife tikupeza, ndiye, kuti zinsinsi izi zikuyenera kuti ziwululidwe.

⁵⁵ Ndipo bwanji sanatero amuna ena awa, Wesile, Lutera, ndi okonzanso opambana awo, amene anatulutsa kulungamitsidwa, kuyeretsedwa, m’badwo wa chipentekoste ndi ubatizo wa Mzimu Woyera ndi zinthu, bwanji iwo sanagwire izi—Mawuthenga awa? Bwanji iwo sanawapeze Iwo? Chifukwa iwo anali okonzanso. Mukuwona?

⁵⁶ Monga ngati, chitengereni icho ku mbali ina, apo panali anthu amene analowamo amene anali “anali nayo mphamvu monga mafumu, koma sanali mafumu.” Mukuwona? Mukuwona? Inu muyenera kuzindikira kalongosoledwe ka Baibulo ka chirichonse. Mukuwona? Tsopano yang’anani. Koma, ichi, chifukwa chimene mbali zonse zosocherera, za gawo la chinsinsi cha kulungamitsidwa, gawo la chinsinsi cha kuyeretsedwa, gawo la chinsinsi cha ubatizo wa Mzimu Woyera. Ndipo, chifukwa, mtundu wanji umene. . . Kodi Eva anadya apulo, kapena kodi iye anadya garagadeya, kapena chinachake? Mukuwona? Kodi. . . Kodi mbewu ya serpenti inali chiyani? Ndipo—ndipo kodi ubatizo mu dzina la “Atate, Mwana, Mzimu Woyera,” kapena Dzina la “Ambuye Yesu,” ndiwo wolondola? Ndipo, o, mazana a zinthu zimenezo, zakhala zitasiyidwa za mapeto-omasuka. Mwawona?

⁵⁷ Ndiyeno mu ora lotsiriza, munthu uyu ali woti abwere ndi kuwulula chinthucho, onani, kuwatenga Malemba. Izo zidzazindikiridwa moyenera. Yang’anani. Inde, bwana. Ndipo, tsopano, icho sichikhala chopambana, chinthu chachikulu tsopano. Icho chimawoneka ngati, apa mu Baibulo, icho chikanakhala chinachake chachikulu.

58 Zinali zazikulu bwanji izo, pamene Yohane ankayenera kubwera pansi kumeneko ndi kudzabatiza! Tangoganizani tsopano. Aneneri, mmbuyo, njira yonse mmbuyo, Yesaya, Malaki, ndi onse a iwo analankhula za iye, pamene iye akanabwera. Ndipo pamene iye anatero, yekha basi, wokalamba, munthu wosaphunzira, ndi ndevu kumaso kwake konse, ndi tsitsi chang’alang’a ngati chiyabwe chosawoneka bwino, ndi chidutswa chachikulu cha chikopa chankhosa chakale chitaphimbidwa chomukuta iye; wopanda maphunziro konse, sanapite konse ku sukulu tsiku la mu moyo wake, monga momwe ife tikudziwira. Mwawona? Apa iye akubwera, kuchokera kuchipululu, osati ngakhale zochuluka monga kulandiridwira ku guwa, ndipo anayima panja apo pa mtsinje wa Yordani ndipo anayamba kuyitanira anthu kuti alape. Mukanakhoza inu kulingalira!

59 Baibulo linanena, kuti, “Chirichonse chidzakhala chopambana kwambiri mu tsiku limenelo, ngakhale mpaka malo onse okwera adzapangidwa kukhala otsika, ndipo malo onse otsika adzakhala okwezedwa.” Inde bwana. “Ndipo malo onse okumbika adzakhala osalazidwa.”

60 Chifukwa, ine ndikhoza kulingalira ndikuwawona iwo kunja uko, kumaganiza kuti Yohane akanatulukira, kapena wotsogolera kudza wamkulu uyu wa Khristu, ndipo kungotenga chipululu chonse ndi kuchisalaza icho, ndi kuyikamo udzu kachiwiri. Mwawona? O, iwo, ine ndikulingalira iwo anali nazo izo zonse zitakonzedwa, pafupi monga iwo ali nazo lero.

61 Koma, izo zinali zodzichepetsa kwambiri, ngakhale atumwi anachiphonya icho. Iwo anati, “Chabwino, bwanji Lemba limati, ngati...Inu mukupita kumeneko kukaperekedwa tsopano? Bwanji Lemba limanena kuti—kuti Eliya ayenera kubwera poyamba?”

62 Iye anati, “Iye wabwera kale, ndipo inu simunadziwe izo. Ndipo, Mwana wa munthu, iwo adzachita chinthu chomwecho. Koma, Yohane,” Iye anati, “anachita basi zimene zinayikidwa kwa iye kuti akazichite. Ndipo,” anati, “koteru ayenera Mwana wa munthu kuzunzidwa.”

63 Bwanji, apo panalibe, ine ndikuganiza, gawo limodzi mwa atatu la mtundu wonse wa Ayuda silinadziwe konse kuti Yesu Khristu anali pa dziko lapansi. Sanati...Iwo mwina anamva za wotentheka wina cha kumusi kumeneko penapake, koma iwo sanapereke chidwi chirichonse kwa izo, amangopitirirabe. “Iye anabwera kwa Ake Womwe, ndipo Ake Womwe sanamulandire Iye ayi.” Tsopano, apo pali pamene ine ndikuhulupirira ngakhale...Tsopano, iwo sananene kuti Iye akanadzabwera mwachinsinsi.

64 Koma Mkwatulo udzakhala chinsinsi. Koteru ngati icho chinali chinsinsi choteru, pamene Iye anabwera, mochuluka

koposa bwanji udzakhale Mkwatulo wosadziwika! Mwawona? Iwo sadziwa izo. Molunjika iwo adzati, “Chabwino, ine ndinaganiza ife timayenera kukhala nawo Mkwatulo. Nanga chiweruzo chonse ichi pa dziko lapansi?”

⁶⁵ Iye adzati, “Iwo wachitika kale, ndipo inu simunadziwe izo.” Mwawona? Izo zidzakhala chomwecho, monga ngati wakuba usiku.

⁶⁶ Monga b—bukhu lomwe ine ndinawerenga, nthawi imodzi. Kodi ilo limatchedwa chiyani? Romeo ndi Juliet, kodi ndicho chimene ilo linali, kapena chinachake? Iye analola, anakweza makwerero apo pambali pa nyumba, njira yina. Ine nd-... Yakhala nthawi yayitali kalekale. Ndipo kubwera, anatenga ake. . . kuti akamutulutsire iye kunja pa nthawi ya usiku.

⁶⁷ Tsopano, ndiyo njira imene iwo udza—iwo udzachtikire, ndipo udzakhala utapita. Osati, iwo adzatumiza gulu la Angelo pansi, ndi makasu ena, ndi kukumba manda. Baibulo linati, “Ife tidzasinthidwa, iwe usanati ngakhale ukanakhoza kuphethira diso lako.” Nkuthwanima kokha, zonse zidzakhala zitatha, mwamsanga choncho.

Mudzangoti, “Winawake wasowa.”

⁶⁸ Chabwino, ine ndikhoza kuganiza ngati ife tikanakhoza kufufuza dziko lonse, lero, pakanakhala anthu mazana asanu osowa pa dziko lapansi tsiku lililonse, onani, iwo sakudziwa kanthu za izo. Iwo akungopezeka, akusowa.

Chabwino, sipakhala ochuluka kwambiri kupita mu Mkwatulo.

⁶⁹ Tsopano, ine sindikufuna kukuwopsyezani inu, ndipo ine—ndipo ine—ine—ine—ine sindikuganiza kuti ziri mwanjira imeneyo, koma ine ndikungofuna kukuwuzani inu zimene Iye ananena. Ndipo inu mukudziwa zimenezo, inunokha. “Monga izo zinaliri mu masiku a Nowa, mmene miyoyo isanu ndi itatu inapulumuka mwa madzi. Miyoyo isanu ndi itatu kuchokera m’dziko, kukhala itapulumuka mwa madzi.”

⁷⁰ Chabwino, inu mukuti, “O, mai! Palibe chifukwa chakuti ine ndiyesere.” Izo zikusonyeza kuti inu mulibe mtundu wa chikhulupiriro umene inu mukusowa.

⁷¹ Ngati kuti kungokhala—kuti kukhale mmodzi, ameneyo adzakhala ine, ameni, chifukwa ine ndikukhulupirira. Mwawona? Ndimo momwe inu mukufuna kuti mukhulupirire izo, onani, “Akhale ine.” Ndithudi. Ine ndikufuna kukhala pafupi kwambiri kwa Iye, kuti ine ndidziwe kuti Iye akudzanditenga ine pamene Iye akubwera. Ine ndikukhulupirira zimenezo. Ndiko kulondola. Kotero ngati pali. . . Ngati wina aliyense awuphonya iwo, ine ndidzakakhala ndiri kumeneko, mwa chisomo Chake. Chifukwa, Iye anandilonjeza ine izo, ndipo ine ndikudziwa kuti ine ndidza—ine ndidzakhala kumeneko,

chifukwa Iye sanganame. Ndipo ine ndikudziwa moyo wanga ndi umoyo zikuchitira umboni, ndipo ine ndikuyesa kukhala moyo tsiku lililonse monga ngati kuti Iye amabwera, kotero ndiri—ine ndidzakhala mmodzi ameneyo. Ndimo momwe iwe ukufuna kumverera, “Ngati pati pakakhale asanu ndi atatu, ine ndidzakhala mmodzi wa asanu ndi atatu awo; akati akakhale mazana asanu, ine ndikakhala mmodzi wa mazana asanu amenewo. Sindikudziwa za munthu wina, koma ine ndikufuna kukhala mmodzi wa mazana asanu amenewo.” Mukuwona? Ndimo momwe inu mukufuna kumakumbukilira. Mwawona?

⁷² Ndipo ngati inu simukukumbukira icho monga choncho, pali chinachake cholakwika nacho chikhulupiro chanu. Mwawona? Inu simuli otsimikizabe kuti mwapulumutsidwa panobe, ndiye. Inu mukulingalira chabe pa icho. Musati muchite izo. Chabwino.

⁷³ Ife sitilowa mu Chisindikizo ichi, si choncho? Chabwino. Ine ndikufuna, usiku uliwonse. . . Ine sindikudziwa kaya inu mudandawula nane kutenga nthawi yanu. Ife tikhoza kutuluka mofulumirirapo pang’ono. Palibe zambiri ayi. . .

⁷⁴ Mu kuwulula kwa izi, kwa Zisindikizo izi, kumbukirani, ndicho kwenikweni ndime imodzi yokha. Yoyamba, ikunena kulengeza kwa icho, ndime yachiwiri. Pafupi ndemanga zonse, ndi zina zotero, kuwerenga kwa izo, kapena—kapena kuwerenga kwa maganizo awo, ndipo ine ndakhala—ndipo ine ndakhala nthawizonse ndikukhulupirira monga pafupi onse a iwo amachitira, kuti wokwera pakavalo woyamba uyo anali—unali mpingo woyambirira. Koma pamene Mzimu Woyera unawulula icho, icho chinali mwamtheradi chosiyana kwa izo. Ndipo kotero ndiye, zonse zimene chimachita, chimangosonyeza chimene icho chiri. Ndiyeno ine ndiyesera. . .

⁷⁵ Tsopano, kwa ine, ichi chiri chopatulika kwambiri. Ndicho chifukwa chake kuli bwino ndiyankhe mafunso awa. Ndipo tiyeni tizitenge izi, aliyense akudziwa mowongoka, ndi pa matepi, naponso, kuti iwo adzamvetse tsopano. Mukuwona? Ine ndinayesa kulankhula kanthawi, mu usiku, pa kuyika maziko, kuwatenga anthu. . .

⁷⁶ Kuthamangira mkati ndi kukankhirana mkati, ndipo, inu musamachite zimenezo. Mukuwona? Koma, pamene izo zitero, ndi anthu okhalapo. Ndipo muli kutentha mkati—mkati muno, ndipo inu—ndipo inu muli osimidwa.

⁷⁷ Koma inu mwakhala kwambiri, abwino kwambiri. Mopambana mmene ndawawonerapo anthu akuchitira, mu kachisi, akhala ali msonkhano uno; ndipo kukhala chete, ndipo amayi kuwatengera ana awo kokawayamwitsira pamene iwo amayamba kulira. Ndipo chirichonse chakhala chiri chabwino kwambiri.

78 Koma ine ndikuyesa kuyikira maziko icho mpaka ine nditangomverera kudzoza kwa Mzimu pa ine, kuti ndinene Mawu awa, kuti ndinene zimene zawululidwa kwa ine. Ndiyeno ngati ine ndikhala, penapake, ndikuchita zimenezo, ngati ine ndalakwitsa apa, ndithudi apa pamaso pa anthu onse Iye adzandikonzera chimenecho ine. Ine—ine ndikufuna icho. Ndicho—ndicho. . . Ine ndikufuna Icho molondola. Palibe chifukwa chotengera chabe zimene iwe ukulingalira. Pali chinachake cholondola, ndipo—ndipo ife tikufuna Chimenecho. Ife tikufuna Mulungu atipatse ife chimene chiri cholondola.

79 Kotero tsopano ife tinatenga awa, okwera awa, pamene iwo akubwera. Kavallo woyamba, tsopano, ndipo ife tikuzindikira kuti ameneyo anali—wotsutsakhristu amene anapitaapo. Ndiyeno ife tinapeza, usiku watha, kuti munthu yemweyo amene anapita apo monga wotsutsakhristu, monga kavalo woyera, ife tinamupeza iye ali nalo lupanga, usiku watha, atakwera, ndi kumapha anthu.

80 Tsopano, tsopano, nthawizonse pali zachirengedwe ndi zauzimu. Ndipo chifukwa cha Mpingo, ine ndikufuna kufanizitsa, ife tisanafike kumene ku kutsegula kwa Chisindikizo ichi.

81 Chimene, chomwe Iye wandipatsa ine, ine ndalembe izo apa. Ine ndiri nawo Malemba angapo apa, masamba asanu ndi awiri kapena asanu ndi atatu a izo, ndipo pamene ine ndikuloza kwa izo.

82 Zindikirani, ine ndikufuna kupereka choyimira, cha Mpingo, ndi kuzipanga izo momveka kwambiri mwakuti inu mudzakhala okakamizidwa kuziwona izo. Mukuwona?

83 Tsopano, panali mkwatibwi wachirengedwe mu munda wa Edeni. Mukukumbukira usiku watha? Mkwatibwi wachirengedwe uyo, iye anali wokomamtima wa Adamu, asanakhalebe mkazi wake, chifukwa iye anali asanamudziwebe iye ngati mkazi wake.

84 Monga ngati Maria anali mkazi wa Yosefe, koma iye anali asanamudziwebe iye. “Iye anapezeka ali ndi mwana.” Mukuwona?

85 Tsopano, Adamu asanamudziwe mkazi wake, iye anali chabe mkwatibwi kwa iye. Chabwino. Ndipo ife tikupeza apo kuti Mulungu. Mkazi, mkazi anagwa mu munda wa Edeni chifukwa iye analephera kugwira ku Mawu a Mulungu.

86 Tsopano, Iye ankadziwa kuti Satana akanadzakhala atamasulidwa pakati pa iwo, kotero Iye anawapatsa iwo—malo kuti azikhala kuseri; kuwatetezera iwo. Chabwino, apo, ndani amene akanakhoza kudziwa malo abwino aliwonse woti akhale wotetezedwa, kuposa Mulungu, ngati Iye akuyesera kusamalira ana Ake omwe?

⁸⁷ Ngati ine ndinafuna kusamalira mwana wanga wamng’ono Joseph, chabwino, m’bale, chirichonse. . . Ndipo ine ndikudziwa kuti moyo wake umadalira pa icho, chifukwa, ndikana. . . ndipo ine ndinali wokhoza kuchita icho. Chabwino, ngati konkire ya mapazi makumi anayi, yolimbikitsidwa, ikanakhala—ikanakhala chinthu chimene chikanachita icho, ndicho. . . Ine ndikanachipanga icho mapazi makumi asanu ndi anayi, kuti ndikhale wotsimikiza, izo.

⁸⁸ Ndipo ngati ine ndingakhoze kuganiza izo pa za mwana wanga wamng’ono, (chimene, ngati moyo wake wachivundi ukanatayika, ine ndikukhulupirira mwanayo akanakhala wopulumutsidwa,) kuli mochuluka bwanji, kwa Mulungu, kwa mwana Wake amene akanakhala wotayika Kwamuyaya! Kodi Iye amuyike iye kuseri kwa chiyani? Iye anamuyika iye kuseri kwa Mawu Ake Omwe. Malingana ngati iwe uli mu Mawu amenewo, iwe uli wotetezedwa. “Ngati inu mukhala mwa Ine, ndi Mawu Anga mwa inu, ndiye mungopempha chimene inu mukufuna.” Ndizo izo, Mawu.

⁸⁹ Koteru, Eva anapita kukayenda mu munda, ndipo iye anakomana ndi serpenti, munthu wokhala ngati wopukutidwa kwambiri. Ndipo iye. . . Ndipo iye kuyamba. . . Tsopano, iye anali ku mbali yina. Mulungu amakhala, amawusa, amagwira ntchito mu kuphweka, osati conse njira yina iliyonse. Mwawona? Tsopano, wamng’ono, dona wodzichepetsa akuyenda motsatira pamenepo, ndipo Satana anabwera apo ngati wanzeru, wothyathyalika, munthu wokhala ngati wopukutidwa. Ndipo iye ankafuna kumugulitsa iye dongosolo. Malinga ngati. . .

⁹⁰ Zinalibe kanthu kaya Satana anali pafupi bwanji; malingana ngati iye akanakhala kuseri kwa Mawu awa, iye anali bwino yense. [M’bale Branham asisita Baibulo lake—Mkonzi.] Mukuwona? Koteru, Msiyeni Satana achite zirizonse iye akufuna kutero; inu mungokhala nawo Mawu. Sizipanga kusiyana kwakung’ono.

Ngati iye ati, “Bwanji, iwe ukudwala.”

“Ndi mikwingwirima Yake ine ndachiritsidwa.”

“Chabwino, iwe ukukafa.”

“Iye adzandizutsa ine kachiwiri. Iye analonjeza izo.”

⁹¹ Onani, ingokhalani kuseri kwa Mawu. Ndizo zonse. Khristu ankabwerera ku Mawu, Iyemwini. “Izo zinalembedwa.” Mwawona? Tsopano, khalani kuseri kwa Mawu.

⁹² Koma, Eva, iye anayamba kukhala ngati kulekerera, koma iye sanalekerere iwo wonse. Iye analekerera chabe ganizo limodzi laling’ono. Ndipo ndicho chimene Satana ankafuna kuti iye achite. Iye anamuchotsa iye kuseri kwa lonjezo la Mulungu mwa kulingalira.

Musati muyesere konse kulingalira Mawu a Mulungu. Ingowakhulupirirani Iwo! Mwawona?

⁹³ Kotero, iye anatuluka nachoka Kumeneko. Ndipo Adamu asanafike konse kwa iye, kukhala mkazi wake, iye anali kale atayipitsidwa ndi Satana. Ndipo iye. . .

⁹⁴ Ndipo kodi inu munazindikira? Khristu anachita chinthu chomwecho, chimodzimodzi. Tsopano, pa kuwombola, Mulungu anayenera kukhala pamenepo poyamba. Kodi inu munazindikira? Mariya, iye asanafike kwa Yosefe, Mzimu Woyera unali utafika kale pamenepo. Amen. Mwawona? Ndipo pamenepo Wowombola akubwera.

⁹⁵ Tsopano, tsopano zindikirani, mkazi wachirengedwe anagwa, ndipo Mulungu anapanga njira kuti iye akhale wowomboledwa. Ngakhale iye anali atagwa, Iye anapanga njira.

⁹⁶ Tsopano, ameneyo anali mkwatibwi woyamba pa dziko lapansi, anagwa, asanati mwamuna wake ndi iye akwatirane. Iye anagwa, mwa—mwa chifukwa cha—cha kulingalira, mmalo mwa kukhala nawo Mawu. Iye anagwa. Ndipo iye anagwera ku imfa, kusiyana Kwamuyaya. Ndi iye, iye anamutenga mwamuna wake ndi china chirichonse chimene chinalipo pa dziko lapansi. Iye anagwa!

⁹⁷ Tsopano, koma, Mulungu, wodzaza chifundo, anapanga njira kuti akamuwombole mkazi ameneyo. Ndipo tsopano Iye anamulonjeza iye, kumuwuza iye kuti nthawi yina, mu tsogolo, Mawu owona akanadzabwera kwa iye kachiwiri. Mawu owona adzapangidwa kudziwika kwa iye. Tsopano kumbukirani icho. Chifukwa, Iye analonjeza Khristu, kupyolera mwa mkazi.

⁹⁸ Ndipo Khristu ali Mawu. Yohane Woyera 1, “Pachiyambi panali Mawu, ndipo Mawu anali ndi Mulungu, ndipo Mawu anali Mulungu. Ndipo Mawu anakhala thupi,” onani, “ndi kukhala nafe ife.” Mulungu anakhala ndi ife mu thupi. Iye anali Mawu.

⁹⁹ Asanakhale Mawu, ali ganizo. Ndipo ganizo liyenera kulengedwa. Chabwino. Kotero, maganizo a Mulungu anakhala chirengedwe pamene iwo analankhulidwa, mwa mawu. Ndipo pamene Iye apereka iwo kwa—kwa inu ngati ganizo, ganizo Lake, ndipo ilo lawululidwa kwa inu. Ndiye, likadali ganizo mpaka *inu* mutalankhula ilo. Ndicho chifukwa. . .

¹⁰⁰ Mose anapita kukapemphera. Lawi la Moto lija pomuzinga iye, ndipo Iye anati, “Pita, ukagwire ndodo yako moyang’anitsa kummawa, ndi kunena, kayitanitse ‘ntchentche.’”

¹⁰¹ Apo palibe ntchentche. Koma iye anapita ndipo anakagwira ndodo kumeneko, ndipo anati, “Lolani pakhale ntchentche.” Palibe ntchentche nkomwe, apobe. Anabwererabe mmbuyo. Koma mawu, ganizo la Mulungu, akhala atalankhulidwa kale. Iwo ali mawu, tsopano icho chiyenera kuchitika.

102 Tsopano kodi inu simukuwona pamene Yesu ananena? “Ngati inu munena kwa phiri ili; osati ngati Ine ndinena icho. Koma *inu* munena kwa phiri ili, ‘Sunthidwa.’”

103 Ndipo chinthu choyamba, ine ndikuganiza, mu nthawi ya Mose, ntchentche yayikulu yakale yagirini inayamba kulira. Ndipo, patapita kanthawi, izo zinali mapawundi asanu pa yadi. Mwawona? Kodi izo zikanachokera kuti? Iye... Mulungu anzirenga izo. Kodi inu simukuwona momwe... .

104 Mulungu akhoza kuwononga dziko ili usiku uno, ndi—ndi atongole, ngati Iye akufuna kutero. Chabwino, Iye akanakhoza kuwunjika atongole mpaka ku mwezi. Chinthu chokhacho Iye akanakhoza kuchita ndicho kungoti, “Lolani pakhale atongole, mpaka ku mwezi.” Icho chikanakhala chonse chomwe chikanakhala kwa icho. Popanda zosakaniza kapena kanthu kena, iwo akanangokhala akukula, kukula, kukulirabe. Mwawona?

105 Iye akhoza kuchita chimene Iye akufuna kuchita. Iye ali Mulungu, Mulengi. Chinthu chokhacho choti achite ndicho kulankhula chabe izo. [M’bale Branham akukhwatichitsa chala chake kamodzi—Mkonzi.] Ndiko kulondola. Iye ali Mulengi. Tsopano, ngati ife tifika chabe pozindikira momwe Iye aliri wamkulu! Mwawona? Iye amachita kokha zimene Iye akufuna kuchita.

106 Iye amakhala pamenepo ndi kumayang’ana pa anthu, ndipo ophunzitsa ang’ono awa, kufuna kuchenjera, ndi, “Kulibe Mulungu,” ndipo—ndipo chirichonse. A! Chifukwa, izo zangokhala ngati iwo anali ku Babulo, kachiwiri. Babulo, kani.

107 Tsopano ife tikuzindikira kuti Mulungu anamuwuzwa Eva, kuti, “Patapita nthawi yotalika chotere, Mawu akubwereranso kwa iwe.” Tsopano, anagwa bwanji iye? Ine ndikufuna kalasi langa linene icho. Iye anagwa ku chiyani? Eva anagwa ku chiyani? Mawu. Kodi nkulondola uko? [Osonkhana, “Mawu.”—Mkonzi.] Mawu. Ndipo Mulungu anati Iye akanapanga njira kuti amuwombole iye kubwerera ku Mawu kachiwiri. Chabwino. Patapita nthawi yotalika chotero, Mawu akanadziwitsidwa kwa iye. Chabwino. Mawu akanabwerera kwa cholinga chimodzi tsopano. Gwirani zolimba tsopano, chimene ine ndikunena. Mawu akanabwera kwa iye kwa cholinga chimodzi, chimenecho chinali kwa chiwombolo. Chabwino.

108 Koma, mpaka—mpaka pamenepo, iye anali nacho choloweza mmalo chimene chikanati—chimene chikanagwira ntchito mpaka nthawi itafika ya Mawu apachiyambi. Tsopano inu—inu mukumvetsa bwino? [Osonkhana, “Ameni.”] Mwawona? Iye anamuwuzwa iye kuti Mawu akanabwera kwa iye kachiwiri, koma, mpaka nthawi imeneyo, Iye anamupatsa

iyе choloweza mmalo mpaka nthawi imeneyo itadzafika. Kotero, Iye anamupatsa iye chopereka kuti apange, choloweza mmalo mwa Magazi aja.

¹⁰⁹ Tsopano, magari anali a ng’ombe ndi nkhosa, ndi mbuzi ndi zinthu, koma iwo sankachotsa tchimo lake. Mwawona? Iwo ankangophimba tchimo lake. Iwo sankalichotsera ilo kutali, konse. Iwo ankaliphimba ilo. Pakuti, iwo anali magari a nyama, ndipo mu magari a nyama muli moyo wa nyama. Iwo anali choloweza mmalo mpaka chenicheni. . . Tsopano valani majekete anu.

¹¹⁰ Magazi enieni, a munthu, monga anthu okhalapo akanakhallira, kukhala mu thupi (Mulungu); popanda kugonana, namwali, kubadwa mwa namwali kunapereka chimenecho. Tsopano Mawu a Mulungu, lonjezo, anadzakhala Magazi, ndipo anadzakhala mu thupi mwa Munthu wa Yesu Khristu Mpulumutsi. “Magazi a ng’ombe ndi mbuzi, ndi zina zotero. . .”

¹¹¹ Koma tsopano dikirani. Apa Mulungu anapanga lonjezo, kunena kuti chidzakhala pamenepo pamene Icho chibwera, “Mbewu yake iyenera kuvulaza mutu wa serpenti.” Tsopano, ngati mbewu yake ingobwera monga kuchokera kwa Adamu, kapena monga iyo inakhallira kuchokera kwa serpenti, ndi zina zotero, ndiye iyo ikanadzakhallabe mbewu yamachimo.

¹¹² Ndicho chifukwa chake Yohane analira. Apo panalibe munthu, chifukwa palibe munthu. . . Aliyense anali atawoloka, mbali yina ya dzenje, phompho. Koma apo pakubwera nthawi imene pamene magari oloweza mmalo a nyama awa akanakhala atathetsedwa, pamene enieni, Magazi okhala mu thupi anabwera: Mulungu, atapangidwa mnofu ndi Magazi. Baibulo linati Iye anali. Timoteo woyamba 3:16, “Popanda kutsutsana chachikulu chiri chinsinsi cha umulungu: pakuti Mulungu anawonetseredwa mu thupi.” Ndiko kulondola. Kubadwa kwa namwali kunachita zimenezi.

¹¹³ Tsopano, magari a nkhosa ndi mbuzi ankaphimba tchimo, koma iwo sankalichotsa ilo, pakuti iwo anali magari a nyama. Koma iwo anali oti zikhale bwino, anali oti akhale choloweza mmalo.

¹¹⁴ Ndipo iwo ndithudi anafika—anafika pozolowera choloweza mmalo icho, ndipo kotero iwo ankangopitirirabe.

¹¹⁵ Ndipo, pamene, enieni, Mawu olonjezedwa anawonetseredwa mwa Yesu Khristu, Yemwe anatsimikizira kukhala Mwana wa Mulengi wamkulu, Mulungu; ndipo anatsimikiziridwa, Iyeyekha, pakukhala Mawu amoyo a Mulungu. Psyi! Mai! Iye anatsimikizira kuti Iye anali. Iye anakhoza kulankhula zinthu nkukhalapo.

¹¹⁶ Apo palibe munthu wokhalapo, kapena—kapena palibe kanthu mu dziko, kakanakhoza kuchita zimenezo. Palibe chinthu pa dziko lapansi chingakhoze kulenga, koma Mulungu.

Mdierekezi sangakhoze kulenga. Iye ali wosokoneza wa chimene chalengedwa kale, koma iye sangakhoze kulenga. Tchimo liri chabe chilungamo chosokonezedwa. Inu mukudziwa chimene ine ndikutanthawuza. Bodza ndi chiyani? Ndiro choonadi cholankhulidwa mokhota. Mwawona? Chigololo ndi chiyani? Kachitidwe koyenera kololezedwa kosokonezedwa. Chirichonse mu tchimo, tchimo liri chabe Choonadi chosokonezedwa. Tsopano, iye sakanakhoza kulenga.

117 Koma pamene Khristu anabwera, anatsimikizira kuti Iye anali Mulengi. Apo panali Magazi amene anali atalonjewedwa. Tsopano ngati inu mukufuna kuwerenga zimenezo, inu... Tiyeni titsegule chabe kwa miniti. Ife titenga nthawi pa izi, chonchobe, usiku uno. Ine . . .

118 Ichu chikundipangitsa ine manjenje. Ine ndikuganiza aliyense akufuna kupita kwawo, inu mukudziwa. Ndipo kotero ziri... [Osonkhana ati, “Ayi.”—Mkonzi.] Tsopano tiyeni tipeze Machitidwe 2. Zikomo inu. Ndipo ife tidzango. . .

119 Machitidwe 2, ndipo ife tidzapeza kaya izi ziri zolondola, kapena ayi, kaya Iye anatsimikiziridwa kuti Iye anali Mulungu. Chabwino. Tipeze Machitidwe 2. Tsopano tiyeni tifike apa pa ndime ya 22, Petro akulankhula, Tsiku la Pentekoste.

Amuna inu a Israeli, mverani mawu awa; Yesu waku Nazareti, mwamuna wotsimikiziridwa ndi Mulungu pakati pa inu mwa zozizwitsa... zodabwitsa ndi chizindikiro, zimene Mulungu anazichita mwa iye pakati pa inu, monga inu wanu- . . . no- . . . inu eniakenso mukudziwa:

120 “Mwamuna amene anatsimikiziridwa, kuti anali Mulungu pakati pa inu.” Mwa zinthu zomwezo zimene Iye anazichita, anatsimikizira kuti Iye anali. Apa pali Petro, akuyimirira pa Sanhedrin, kuwawuza iwo.

121 Nikodemo anadziwa mofanana. Iye anati, “Mphunzitsi, ife tonse tikudziwa kuti Inu ndinu mphunzitsi wochokera kwa Mulungu, chifukwa palibe munthu amene akanakhoza kuchita zinthu izi pokha Iye atachokera kwa Mulungu.” Mwawona? Iwo ankadziwa zimenezo. Koma bwanji?

122 Tsopano yang’anani. Tsopano, Eva analonjewedwa ichi. Koma pamene . . . Mkwatibwi ameneyo anabwera mpaka pansu, ndipo anakana, pamene Mawu enieni anabwera kwa iye. Kotero, mkazi anakana kuti azindikire; Mkwatibwi Wachihebri. Pakuti, iye anali mkwatibwi wa—wa Mulungu; Iye anamusiya iye, mwa chilekano. Kodi nzoona zimenezo? Iye anali mkwatibwi wa Mulungu.

123 Inu mukuti, “Chabwino, iwo anali asanakwatirane konsebe.” Ndiko kulondola. Koma Yosefe anamusiya Mariya asanati... Anali kukamutsudzula Maria iwo ali asanakwatirane. Mwawona? Iye anatomeredwa kwa iye.

124 Ndipo pamene Iye anabwera, ndipo Mawu amene Iye anawalonjeza, anabwera kudzakwatitsa, Iye anamupeza iye atakutidwa mu zoloweza mmalo zake, moyipa kwambiri, kuti iye sakanatenga lonjezo lenileni limene linali litapangidwa, Mawu, Khristu.

125 Mwinamwake inu simuzikumvetsa izo. Tsopano ndiroleni ine ndibwereze zimenezo kachiwiri. Ine ndikufuna inu kuti mumvetse izi, onani.

126 Iye anali atalonjezedwa, (mkwatibwi, Eva), kuti kukhale Wowombola. Wowombola wake akanakhala Mawu. Ndipo pamene Mawu anabwera, kupangidwa thupi, iye anawakana Iwo. Iye apatsidwa zoloweza mmalo. Tsopano gwirani chimenecho, “choloweza mmalo.” Anapatsidwa zoloweza mmalo kuti azipitirirabe, mpaka Wowombola abwere. Ndipo pamene Wowombola abwera, iye ankafuna kuti azipitirira nacho choloweza mmalo chake, ndipo anakana Mawu owona. Mwawona icho? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Ndipo ameneyo anali mkwatibwi wa Chihebri.

127 Koteronso anachita Iye, mwa Eva wachiwiri, mkwatibwi, mayi wa zonse zamoyo zauzimu. Mwawona? *Eva* amatanthawuza “mayi wa onse,” zomwe ziri mzimu-. . . “onse amene ali amoyo.” *Eva*, “mayi wa onse amene ali amoyo.”

128 Tsopano, ndipo pamene Iye anabwera kwa mkwatibwi wa Chihebri, iye anali mayi wa onse amene anali amoyo, koma iye anawakana Iwo.

129 Eva wachirengedwe anagwa, mu Edeni, pa kumvetsera ku kulingalira kwa Satana kotsutsa Mawu a Mulungu. Ndimomwe iye anagwera. Chabwino, bwana. Iye anagwa chifukwa iye anachita izo.

130 Eva wauzimu, tsopano, ndiwo Mpingo, mkwatibwi wa Khristu. Iye anagwa, osati mu Edeni, koma mu Roma, onani, pa Khonsolo ya Nicaea, pamene iye anakana. Mpingo wa chipentekoste uwo umene unapita mpaka ku Nicaea, ndi kumvetsera ku kulingalira kwa Roma, mmalo mogwiritsa ku Mawu, iye anagwa. Ndipo zirizonse za kutali kwa iye, zinafa naye iye, pomuzungulira iye. Tsopano, monga momwe Eva wachirengedwe anagwa, Eva wawuzimu anagwa. Mkwatibwi wa Mulungu anagwera—anagwa mu munda; Mkwatibwi wa Khristu anagwa mu Roma. Mwawona?

131 Zindikirani, mwa kulingalira komweko, kotsutsa Mawu a Mulungu, iye nayenso anapinyolitsa maufulu ake a ukoma, kwa Satana. Zomwe, ife tinazipeza mu kumatula kwa Zisindikizo izi, kuti ameneyo anali Satana, ndipo akadali Satana kumeneko. Baibulo linati ndiwo mpando umene wa Satana. Ndipo monga Eva anapinyolitsa wake—maufulu a ukoma wake, ndi kuwapereka iwo kwa Satana, mu munda wa Edeni; mpingo, mkwatibwi wa Khristu, anachita chinthu chomwecho ku Roma,

pamene iwo anapinyolitsa Baibulo kwa miyambi yawo ndi malingaliro. Mukuwona momwe zikuyimira? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.]

132 Inu mungofanizitsa zoyimira zimenezo, inu mpaka mukatulukamo olondola. Ngati dzanja langa likuwoneka ngati...Ngati ine sindinadziwonepo ndekha, ndipo ine ndikuwona chithunzi changa chikubwera, ine ndidziwa basi momwe ine ndimawonekera. Mwaona? Koma, ndiyo njira yake. Ngati inu mukufuna kuwona chimene chikubwera, muyang’ane chimene chakhala chiripo. “Pakuti z...zinthu zonse zakale zinali mithunzi ya zinthu zakudza,” Baibulo linatero. Chabwino.

133 Pakuti, iye anapinyolitsa Mawu ake a ukoma, Mawu a Mulungu, pamene iye anagulitsa Baibulo, ndi kumuyika munthu mmenemo amene amanena kuti mpingo uli nawo ufulu wosintha chirichonse chimene iwo akufuna kusintha. Ndipo iwo achita izo. Ndipo mkwatibwi wa Khristu, mkwatibwi wa chipentekoste, anagulitsa ukoma wake, pa Nicaea, basi momwe Eva anagulitsira ukoma wake kwa Satana mu munda wa Edeni. Chimodzimodzi. Chabwino.

134 Mulungu walonjeza; mpingo uno, mpingo wa chipentekoste uwu, podziwa kuti iwo ukanachita izo; monga Iye anachitira kwa Eva, Mulungu walonjeza.

135 Mpingo wa chipentekoste, kodi inu mukukhulupirira kuti iwo unagulitsa maufulu obadwa nawo ake, usanati... ukoma wake, pamene iwo unachoka cha kumeneko? Inu mukukhulupirira zimenezo? [Osonkhana, “Ameni.”—Mkonzi.] Iwo, zedi, iwo anatero. Ndiye ndi chaubwino wanji chikhulupiriro, chosakhazikika pa Baibulo ili? Ine ndikufuna wina apeze chimene chimatchedwa Chikhulupiriro cha Atumwi, kapena ngakhale liwu limodzi la izo mu Baibulo. Icho ndi chikhulupiriro cha Chikatolika, osati chikhulupiriro cha atumwi.

136 Werengani Machitidwe 2:38, ndicho Chikhulupiriro cha atumwi, ngati Iye ali nacho chirichonse. Eya. Mwawona? Tsopano, ndicho chimene iwo ankagwiritsa ntchito nthawi zonse, mulimonse. Kotero ngati inu...Mwawona?

137 Kotero, iwo anagulitsa mawufulu awo obadwa nawo. Osati awo okha, Amethodisti, Abapatisti, Apresibateria, Achipentekoste, ena onsewo, achita mofanana. Iye anapanga chipembedzo. Roma, chinamupanga iye nchiyani kuti achite zimenezo, iye anapanga chipembedzo ndi kuyika munthu pa ulamuliro wa icho. Ndipo Amethodisti, Abapatisti, Achipentekoste ndi aliyense, achita chinthu chomwecho, kuyika gulu la amuna pa ulamuliro wa icho. Ziribe kanthu chomwe Mulungu akunena, iwo...Iwe uyenera kuchita izo mwa njira yomwe iwo akuti uchitire izo.

¹³⁸ Chabwino, nchiyani chimenecho? Sichina mu dziko koma uhule wauzimu, mkazi wa mtundu wolakwika; inde, bwana, zikhulupiriro, zikhulupiriro zabodza, zopangidwa ndi anthu. Ndiye iye anakhala, pamene iye anachita izo. . . Tsopano ine nditsimikizira ichi. Iye anakhala mkazi wachigololo, kwa Mulungu. Kodi inu mukukhulupirira kuti Baibulo limanena zimenezo? Inde, bwana. Ana ake aakazi achita zomwezo.

¹³⁹ Tsopano mu Chivumbulutso 17, ngati inu mukufuna kuzilemba izo. Yohane anatengedwa mu Mzimu, “Ndipo anawona mkazi wachigololo wamkulu atakhala pa. . .” Ndipo ife tinawerenga zimenezo usiku watha. Ndipo apo panali mapiri asanu ndi awiri, ndipo chimodzimidzi chimene iye anali atachita. Ndipo iye anali atalipatsa dziko ziwerewere zauve zake. Nkulondola uko? “Ndipo mafumu onse a mdziko anachita naye chiwerewere iye,” kunyenga, ndi kuba, ndi kunama, ndi kulipirira kulapa, ndi—ndi kudzitunduzwa, ndi chinthu china chirichonse.

¹⁴⁰ Chabwino, tsopano kumbukirani, iye anali nawo ana aakazi. Chabwino, ngati iye anali atakhala gulu, ndi pansu pa kachitidwe ka bungwe, ndiye kachitidwe konseko kali kolakwika. Ndipo ngati Eva, posamvera Mulungu, anaponyera chirichonse mu imfa, chimene chinali pansu pa iye; ndipo mpingo uliwonse umene ukhala bungwe, umaponyera chirichonse ku imfa, pansu pa iwo. Chimodzimidzi. Chinthu chonse chapita. Ndizo chimodzimidzi malingana ndi Mawu apa. Werengani Chivumbulutso 17. Ndipo Baibulo linanena kuti Iye “adzamuwotcha iye nawo moto, ndi onse a ana ake ndi iye.” Ndiko kulondola. Chimenecho chikutanthawuza, kachitidwe kalikonse ka bungwe kadzawotchedwa, limodzi ndi mkazi wachigololo.

¹⁴¹ Tsopano, izo zikumveka mosabisa, ndipo ine—ine ndikudziwa inu mudzamva kuchokera kwa iyo, ndipo ine—ine ndikufuna ndimve kuchokera kwa iyo. Ndipo ine—ine. . . Ndiko kulondola, ngakhale. Baibulo linanena chotero, kotero izo zimapangitsa ilo kulondola.

¹⁴² Iye anakhala “hule.” Inu mukhoza kuwerenga izo mu Chivumbulutso, mutu wa 17. Iye, kodi iye anachita chiyani? Iye anachita ziwerewere, mosutsana naye Mwamuna wake yemwe. “Chabwino,” inu mukuti, “ayi, ndilo Baibulo.” Mawu ali Mulungu. Ndipo ngati inu mutenga kanthu kamodzi. . .

¹⁴³ Kodi inu mukanafuna mkazi wanu aziopsyopsonana ndi mwamuna wina? Ngati iye sanachite zoposa chimenecho, inu simukanafuna iye kuchita izo. Iye akanatsimikizira kusawona kwake.

¹⁴⁴ “Aliyense amene adzachotse Liwu limodzi kuchokera mwa Ilo, kapena kuwonjezera limodzi kwa Ilo.” Aleluya! Khristu akufuna Mkazi Wake akhale wangwirowo nawo Mawu. [M]bale

Branham akugogoda pa guwa nthawi zinai—Mkonzi.] Ndi momwe Iye ayenera kukhalira.

145 Chifukwa, palibe, osati dontho limodzi, kapena kukhwatsha kumodzi, kapena kalikonse, kapena neno, zidzachoke kwa lamulo limenelo, kapena kuchokera ku Bukhu limenelo, mpaka Izo zonse zitakwaniritsidwa. Yesu anati, “Zonse kumwamba ndi dziko lapansi zidzachoka, koma Mawu Anga sadzachoka konse.”

146 Musati muyike kumasulira kwamtseri kulikonse kwa Iwo. Iye akufuna angwiro, osakhudzidwa, osati ngakhale kudzivula. Ine sindingafune mkazi wanga kumavulira amuna ena. Ndipo pamene inu mupita kukamvera ku malingaliro ena aliwonse, opyola Iwo, inu mukumvetsera, inu mukumuvulira Satana. Ameni! Kodi izo sizikukupangani inu kumverera mwachipembedzo? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Mulungu akufuna inu mukhale osakhudzidwa. Mukhale pomwepo nawo Mawu amenewo. Mukhale pomwepo nawo Iwo. Chabwino.

147 Mulungu analonjeza kwa iye, monga Iye anachitira kwa Eva mu munda wa Edeni, kwa Eva wotsiriza uyu apa. Amene, mpingo wa chipentekoste, chiyambi cha mpingo, mpingo iwowomwe, uli mayi wa onse a anthu amoyo, chifukwa, malingana ngati iwo apita mmenemo. Koma, inu mukuwona, pamene iwo atenga machimo ake, iwo amafa limodzi naye.

148 Apa pakubwera mnyamata wamng’ono motsatira. Iye akuti, “Ine—ine ndikufuna kutumikira Mulungu.”

149 Iwo amati, “Chabwino, apa pali chimene iwe uchite. Pita kumusi uko ndipo kalape.”

“Chabwino, ine ndichita izo. Ulemerero kwa Mulungu!” Kupita kumusi uko, kukalapa.

150 “Tsopano bwera udzatijowine ife.” Apo, apo inu muli. Anha. Mwawona? Icho chiri nazo. A! Ndiko kulondola, amafa nazo izo kumene. Mwawona? Mwawona? Ndizo chabe. . . Ndicho chimene Bukhu ili likuphunzitsa, onani, osati zimene ine ndikunena. Chifukwa, Ilo likunena Apa, chotero. Chabwino.

151 Tsopano, Mulungu wamulonjeza iye, monga Iye anachitira Eva. Iye anamuwuzwa Eva padzabwera nthawi imene—Mawu akanadzabwereranso kwa iye kachiwiri. Tsopano inu mukukumbukira izo? Chimene iye anatayikako, icho chikanakhala chitabwezeretsedwa. Chifukwa, pali Chinthu chimodzi chokha chingakhoze kubwezeretsa, ndipo ndicho Mawu. Chimodzimodzi.

152 Ine ndinati, kuwombera mfuti; ngati iwe siwumenya chandamale, upeze pamene iyo inaphonyera. Iwe uyenera kubwerera mmbuyo pamenepo ndi kuyamba kachiwiri. Mwawona?

153 Ndipo ngati inu mubwerera mmbuyo, inu mupite ku Nicaea. Ndiko kumene inu mukayambe kachiwiri, mwawona. Mupite mmbuyo, kutali ndi mabungwe amenewo, kutali ndi mpingo wonse uwo. Ife takhala tikuwona Zisindikizo izi mwangwiro basi.

154 Ine nthawizonse ndinkadabwa, moyo wanga wonse, chifukwa chimene ine ndinkatsutsanira nawo kwambiri machitidwe a bungwe. Osati anthu, ayi. Anthuwo ali monga ngati ine kapena inu, kapena wina aliyense. Koma kachitidwe ako, kachitidwe ka chipembedzo ako, tsopano ine ndikuziwona izo pomwe apa. Ine sindinkazidziwa izo mpaka tsopano. Ndipo uko nkulondola.

155 Mulungu analonjeza Eva wauzimu, mofanana monga Iye anamchitira Eva wachirengedwe, kuti kachiwiri Mawu akanadzabwezeretsedwa kwa iye. Mu masiku otsiriza Iye akanabwezeretsa kwa Mpingo, ku Mawu apachiyambi kachiwiri.

156 Tsopano yang'anani mwatcheru kwenikweni. Ine—ine ndikufuna inu mukhale otsimikiza tsopano. Mulungu anamulonjeza Eva, nthawi ikanabwera pamene Mawu akanadzabwezeretsedwa ndi Mbewu yake. Mawu awa, Pawokha, akanakhala Mbewu. Ndipo pamene iwo anamupatsa iye choloweza mmalo, iye anagwira choloweza mmalo icho. Ndipo pamene Mawu anabwera kwa iye, iye akanachita chiyani? “Ine sindikuwafuna Iwo.” Iwo anali onyozeka kwambiri. Sanawoneke mwabwino, kwa iye. Sanali opukutidwa mokwanira. “Kholo? O, mai! Mai! Mnyamata ngati ameneyo, wosapita tsiku limodzi ku sukulu? Chabwino, ine sindikanakhoza kulandira Zimenezo. Ameneyo si Mesiya. Mnyamata wolola anyamata ankuzunguza Iye chotero, ndiyeno nkumtcha Ameneyo ‘Mesiya’? Kulola iwo kumuyika chisanza pa nkhope Yake, ndiye kumamumenya Iye pa mutu? Ndipo Iye kumadzitcha Yekha Mneneri, Mneneri weniweni, atawuka?”

157 Makamaka, iwo sankadziwa aneneri. Yesu ananena choncho. Iye anati, “Ngati inu mukanawadziwa aneneri, inu mukanandidziwa Ine.” Ndiko kulondola.

158 Tsopano zindikirani. Koma pamene Mawu anabwera kwa iye, mwanjira, chimodzimodzi momwe Mulungu anati Iwo akanadzabweza; iye anali atawawerengera Iwo mwanjira yina yake. Ine ndikulankhula za mkwatibwi, mkwatibwi wa Chiyuda, mkwatibwi wa Chihebri. Ameneyo anali Eva, kuyamba ndi kuyamba. Ndiye pamene Iwo anatulukira apa, iye sanawafune Iwo. Iye ankafuna kukhala nazo zoloweza mmalo zake.

159 Tsopano, Mulungu anamulonjeza Eva wauzimu, ku Pentekoste, anachinena icho ngakhale icho chisanachitike, zaka mazana anai mpingo usanagwe konse, kuti iwo akanadzagwera kutali, ndipo iwo akanadzachita zimene iwo anachita. Koma,

Iye analonjeza, mu masiku otsiriza Iye akanadzatumiza Mawu kachiwiri.

160 Yesu analankhula chinthu chomwecho pamene Iye anali pa dziko lapansi; Iye akanadzatumiza Iwo kachiwiri. Ndipo chomwe chiri...Kodi Iwo udzapeza chiyani? Iwo udzapeza chinthu chomwecho chimene Iwo anachipeza pamene Iwo anabwera koyamba. Kulondola. Iwo ali nazo...Iwo, iwo akufuna zoloweza mmalo zawo. Iwo akufuna chipembedzo chawo. Iwo akufuna zikhulupiro zawo. Iwo akufuna kukhala moyo basi momwe iwo akufunira kukhala. Ndipo iwo akufuna, “Chabwino, ine ndine *Wakati-ndi-wakati*. Ine ndine wa *kwakuti-ndi-kwakuti*.” Sizimapanga kusiyana kulikonse chimene Mulungu akuchita, kuchuluka kwake momwe Iye amadziwonetsera Yekha; Iye akanakhoza kudzutsa akufa; Iye akanakhoza kutchula zinsinsi za mitima; Iye akanakhoza kuchita chirichonse chimene Baibulo linati Iye akanadzachita. Zimenezo sizimapanga mpang’ono pomwe kusiyana. “Ngati izo siziri zolumikizana nalo bungwe langa, palibe kanthu kwa Iwo.” Mwawona?

161 Chinthu chomwecho chimene Mkwatibwi wa Chihebri anachita, ndiko kulondola, onani, iwo anamvera kwa choloweza mmalo chawo. Ndipo Mulungu anawalonjeza iwo chenicheni. Ndipo pamene chenicheni chinabwera, iwo sanachifune Icho. Icho chinali chonyozeka kwambiri.

162 Tsopano ndicho chinthu chomwecho lero, pamene—pamene Icho chikutulukira powonekera. Tsopano, Mulungu anati, mu Malaki 4, kuti Iye akanadzatumiza Uthenga mu masiku otsiriza, umene ukanadzabwezeretsa. Yoweli anati, “Ine ndidzabwezeretsa zaka zonse.” Chirichonse chimene Roma anadya, ndi chirichonse Amethodisti anachidya, ndi chirichonse Abapatisti anachidya, kuchokera mu nthambi ya pentekoste yapachiyambi, Mulungu anati, “Ine ndidzabwezeretsa mu tsiku lotsiriza.” Ndiko kulondola.

163 Ndipo Iye akhoza kutitumizira ife munthu woteroyo amene ati adzakhale...Chinthu chokhacho chimene Mulungu anatuzimirako konse Mawu Ake chinali mneneri, osati kwa okonzanso; kwa aneneri. Ilo silinali ora la izo. Tsopano ilo likuyandikira kukhala ora, ndipo ndicho chifukwa chake ife tikuyang’anira icho kuti chibwere. Icho chidzakhala chonyozeka kwambiri ndi chofatsa! Ndipo koter... O, mai!

164 Inu mukuganiza awo opezabwino Amethodisti, Abapatisti, ndi Apresibateria, ndi Achipentekoste, adzachilandira konse icho?

“O,” inu mukuti, “Achipentekoste?”

165 Achipentekoste ndiwo Alaodikaya. “Achuma, ndipo alibe kusowa kanthu.”

¹⁶⁶ Ilo linati, “Iwe sukudziwa kuti ndiwe wosawuka.” Ukhoza kukhala ukumamanga manyumba amadola mamiliyoni, koma iwe ndiwe wosawukabe, kusawuka mwauzimu.

“O,” inu mukuti, “Ine ndikuwona Izo zonse.”

“Iwe ndiwe wakhungu!”

“Chabwino,” inu mukuti, “Mulungu adalitsidwe, ine ndaphimbidwa.”

“Wamaliseche!”

“Chabwino, ine ndikutsimikiza za anyamata athu. Ife tiri nawo maseminare. Ife . . .”

¹⁶⁷ “Ndipo sukudziwa izo.” Tsopano ndizo kokha mbali iyi ndi iyo. Tsopano, ngati Baibulo linanena kuti Mpingo wa Laodikaya ukanadzakhala mu chikhalidwe icho . . .

¹⁶⁸ Ndipo palibe munthu pa dziko lapansi akanakhoza kukana kuti uwu sululi m’badwo wotsiriza, chifukwa, M’badwo wa Mpingo wa Laodikaya, kapena, m’badwo wa mpingo wachisanu ndi chiwiri. Ndipo, apa ife tiri, zaka zikwi ziwiri zachiwiri zikutsirizitsa iwo. Palibe mibadwo ya mpingo yina. Ndicho chifukwa chake inu abale a Mvula ya Masika simukanakhoza kuyamba bungwe lina. Sipakhala kuli yinanso. Ndiko kulondola. Iwo uli pa mapeto. Amen. Sikungakhoze kukhala mibadwo ya mpingo yina. Iyo yonse yatha.

¹⁶⁹ Koma ndiye ngati uthenga wa chipentekoste unali uthenga wotsiriza . . . Umene, kulungamitsidwa, kuyeretsedwa, ubatizo wa Mzimu Woyera, mawuthenga atatu otsiriza, mibadwo itatu yotsiriza ya mpingo ikupanga Kubadwa kwathunthu.

¹⁷⁰ Monga ngati pamene mkazi akukhala, ati akhale ndi mwana wake; chinthu chenicheni choyamba chimene chimachitika ndicho madzi, chinthu chotsatira ndi magazi, chinthu chotsatira ndi moyo.

¹⁷¹ Pamene iwo anamupha Yesu pa mtanda, zinthu zinachokera mu thupi Lake, kuti zipange kwatsopano . . .kuti zipange—Kubadwa. Iwo anakantha mu mbali Yake, Magazi ndi madzi anatuluka, ndipo, “Mmanja Mwanu Ine ndikupereka Mzimu Wanga.” Chimene chinabwera kuchokera m’thupi Lake chinali madzi, Magazi, Mzimu.

¹⁷² Tsopano, Yohane Woyamba 5:7 amakuwuzani inu za izo, “Pali atatu amene amachitira umboni Kumwamba, Atate, Mawu (amene ali Khristu,) ndi Mzimu Woyera.” Ndipo atatu awa amagwirizana mu chimodzi; iwo sali mmodzi, koma iwo amagwirizana mu chimodzi. Ndipo alipo atatu amene amachitira umboni . . .Kapena, “Iwo ali mmodzi,” ine ndikutanthawuza. Ine ndalakwitsa pamenepo. “Ndipo zitatu zomwe zimachitira umboni mu dziko lapansi, ziri madzi, Magazi, ndi Mzimu, ndipo izo zimagwirizana mu chimodzi.”

173 Inu mukhoza kuyeretsedwa opanda kulungamitsidwa. Ndipo inu mukhoza kulungamitsidwa opanda kuyeretsedwa. Inu mukhoza kuyeretsedwa opanda kulandira Mzimu Woyera. Ndizo chimodzimodzi.

174 Ophunzira, mu Yohane 17:17, anayeretsedwa ndipo anapatsidwa mphamvu kukatulutsa ziwanda, komabe anali alibe Mzimu Woyera. Mukuwona? Ndithudi. Amayenera kupita pamwamba ku Pentekoste, ndi kukayembekezera mpaka Mzimu Woyera utabwera.

175 Ndipo pamene Yudasi anawonetsera manga ake. Mukuwona momwe mzimu umenewo umapanga njira yake kupyola mu kulungamitsidwa, kuyeretsedwa? Koma pamene izo zinafika pa mapeto, iye anawonetsa manga ake. Mukuwona? Ndiko kulondola.

176 Tsopano zindikirani, tsopano, ndipo apa ife tiri pa nthawi yotsiriza. Ndipo Eva wauzimu, basi monga wac-...monga Eva wa Chihebri analonjezedwa, Mkwatibwi wa Chihebri analonjezedwa Mawu kuti abwerera. Ndipo mkwatibwi wauzimu kuchokera pa Pentekoste, pamene iye anagwa ku Nicaea, ndiye iye walonjezedwa mu masiku otsiriza kuti Mawu adzabwera kachiwiri. Tsopano inu mukuti, ndiye. . .

177 Inu mukufuna Lemba lina, tengani cha apa, Chivumbulutso 10. Ndipo anati, “Mu ora, nthawi ya—mngelo wotsiriza, mngelo wachisanu ndi chiwiri (mtumiki wachisanu ndi chiwiri) akuyamba kuwomba, chinsinsi cha Mulungu chikutsirizidwa.” Mwawona? Kubwezeretsa kubwerera ku Mawu! Baibulo linati kuti mtumiki uyu wa masiku otsiriza akanakhala, “Kuwabwezeretsa iwo kubwerera ku Chikhulupiriro chapachiyambi kachiwiri, kubwerera ku Chikhulupiriro cha atate.” Koma kodi inu mukuganiza kuti iwo achilandira Icho? Ayi, bwana. “Masiku otsiriza, Iye adzabwezeretsa Mawu apachiyambi kachiwiri,” monga Iye ananena mu Malaki 4.

178 Koma iye anali atapinyolitsa. Tsopano, iye anali atapinyolitsa Mawu amenewo ku Nicaea. Eva anapinyolitsa mu Edeni; Eva anakana ake pa Gologota. Ndipo gulu la Nicaea likuwakana Iwo mu masiku otsiriza, mofanana basi. Mai!

179 Koma pamene Mawu anabwera mu thupi la munthu, iye, Eva, mpingo wa Chihebri, mayi wa onse amoyo auzimu, Iwo ndiye, iye anawakana Iwo. Iye anali wakufa kwambiri, mu miyambo yake ndi ziphunzitso, mwakuti iye anawaphonya Iwo. Koteru ali mmodzi uyu, chimodzimodzi. Chabwino.

180 Iwo amamuphonya Iye, Mawu amoyo owonetseredwa mu thupi, mwa Mawu amene alonjezedwa. Mawu analonjeza kuchita zinthu izi. Lonjezo linapangidwa, kuti izo zidzakhala monga chonchi mu masiku otsiriza. “Monga izo zinaliri mu masiku a Sodomu, koteru zidzakhalanso mu Kudza kwa Mwana wa munthu.” Tsopano yang’anani chimene

chinachitika ku Sodomu. “Monga zinaliri mu masiku a Nowa, koteru zidzakhalanso mu kubwera kwa Mwana wa munthu.” Mwawona? Yang’anani zomwe zinachitika ndiye. Mwawona? Tsopano, Iye anati icho chidzakhala chinthu chomwecho, ndipo ife tikukhala mu tsiku limenelo. Chabwino, ndipo izo zikhoza kukhala, ine ndikuganiza, ine ndikhoza kutenga malonjezo mazana asanu ndi amodzi a iwo chotero, kuchokera mu Lemba, kumangofanizitsa kwa iwo. Mwawona? Tsopano, koma, iwo amawakana Iwo.

¹⁸¹ Iye anagwira ku miyambo ndi zoloweza mmalo, mmalo mwa—a...Iye anagwira kwa magari oloweza mmalo, mmalo mwa Magazi enieni. Yesu, Mawu, anati, pamene Iwo anawonetseredwa kwa iye, “Chifukwa iye anagwira ku miyambo iyi...” Yesu, Mawu owonetseredwa, anati kwa mkwatibwi, mkwatibwi wa Chihebri, “Chifukwa inu mukugwira ku miyambo yanu, inu mukuwapanga Mawu a Mulungu kukhala opanda mphamvu kwa inu. Iwo sangakhoze kukhala amphamvu.”

¹⁸² Tsopano ndicho chiri chifukwa lero, kuti, zi—zitsitsimutso zimene ife tikuyenera kukhala nazo, ife tiri nazo zitsitsimutso zachipembedzo. Iye sitinakhale nako kukondoweza kwenikweni. Ayi, ayi, ayi. Ayi, bwana. Musati muganize kuti ife tiri nazo zitsitsimutso. Iye tiribe. O, ali nawo mamiliyoni ndi mamiliyoni ndi mamiliyoni a mamembala a mpingo, koma osati chitsitsimutso paliponse. Ayi. Ayi.

¹⁸³ M—Mkwatibwi sanakhalebe nacho chitsitsimutso. Mwawona? Pakhala palibe chitsitsimutso pamenepo, palibe mawonetsedwe a Mulungu kuti amukondoweze Mkwatibwi panobe. Mwawona? Iye tikuyang’anira chimenecho tsopano. Zidzatengera mabingu asanu ndi awiri awo osadziwika kumbuyo uko, kuti amudzutse Iye kachiwiri, onani. Eya. Iye adzachitumiza icho. Iye analonjeza icho. Tsopano yang’anani.

¹⁸⁴ Tsopano, iye anali—iye anali wakufa. Ndipo tsopano ngati mipingo ikanayiwala zikhulupiriro zawo, ndi kuyiwala miyambi yawo, ndi kutenga chabe Baibulo, kuvomereza lonjezo, ndiye icho chikanabwera champhamvu kwa iwo. Koma, onani, Yesu anati, “Inu, ndi miyambo yanu, mumapanga Mawu a Mulungu kukhala opanda mphamvu kwa inu.” Chabwino, ndicho chinthu chomwecho lero ndi Eva wauzimu, mwawona, mkwatibwi wauzimu wa lero, wotchedwa choncho, mpingo. Iye akutenga Mawu a Mulungu, ndipo iye sawalandira Iwo. Ndipo iye akulandira miyambi, mmalo mwake. Chotero, Mawu sali amphamvu kwa iye, onani, chifukwa iye akuyesera kubayiramo chikhulupiriro chake ndi Mawu, ndipo izo sizigwira ntchito. Tsopano, chimene ife tikusowa lero . . .

¹⁸⁵ Ine ndikungowerengabe ichi apa, *Herald of His Coming*, pa mawu akulu, “Ife tikufuna mneneri kuti abwerere! Ife

tikufuna mneneri kuti abwerere!” Ndipo ine ndikuganiza, pamene iye ati abwerere, iwo sadzadziwa kanthu za icho. Chabe. . . Ndiko kulondola. Izo nthawizonse zakhala mwanjira iyo, inu mukuwona. “Ife tikusowa icho,” chirichonse chimene inu mungachinene, “ife tikusowa mneneri kuti abwerere, amene ati adzabweretse Mawu a Ambuye, wopanda mantha. Ife tikukhulupirira Baibulo linalonjeza izo.”

¹⁸⁶ Tsopano, ine ndikumudziwa M’bale—M’bale Moore ndi iwo, ndadya mu nyumba yake, ndi china chirichonse, mkonzi. Ndipo iye ndi munthu wabwino zedi amene—amene amayenda mu nsapato ya chikopa, ine ndikuganiza, mmodzi wa anthu abwino zedi. Koma, onani, iye akudziwa kuti ife tiyenera kukhala naye uyo. Ndipo Mlongo Moore, mmodzi wa akazi abwino kwambiri, wamng’ono—munthu wamng’ono wosawuka, ndipo iwo amadzipereka.

¹⁸⁷ Ndipo ndiyo imodzi mwa mapepala abwino pa ntchitoyi, mwa lingaliro langa, *The Herald of His Coming*. Koma inu mukupezapo, iwo akupitiriza kufuula zimenezo, “Ife tikusowa mneneri! Ife tikusowa mneneri!” Mwawona? Mai! Ndicho chimene iwo amachikamba.

¹⁸⁸ Ndiyeno apa ife tiri, lero, ndipo monga dzulo ndi lero, kulengeza pa wailesi, kuti. . . ndipo mipingo ya Bapatisti ndi yina yotero, kuti, “Ife sitienera kutengeka nawo Achikatolika, koma ife tizikhala ngati kuyanjana nawo iwo.” Mwawona?

¹⁸⁹ Ndipo pomwe apa, Uthenga ukutuluka pomwe apa, kuti, “Khalani kutali kwa chinthu cha chiphe icho!” Mwawona? Mwawona? “Angayende bwanji awiri palimodzi pokhapo iwo atagwirizana?” Kuwala ndi mdima sizingayanjane palimodzi. Pamene Kuwala kulowa mkati, mdima umatuluka. Mwawona? Izo sizingakhoze. . . Champhamvu kwambiri! Inu simungazimitse Kuwala, ndi mdima. Koma inu mukhoza kuzimitsa mdima, ndi Kuwala. Ndiko kulondola. Ndipo Iye ali Kuwala, ndipo Iye ali Mawu. Mwawona? Tsopano, apo inu muli, kubwerera cholunjika kumene. Inu simungawapangitse Iwo kunama kapena kuchita chirichonse cholakwika. Iwo amabwerera mmbuyo cholunjika kumene ku malowo kachiwiri. Inde, bwana.

¹⁹⁰ Monga ngati munthu wina akayamba, kuyesa kukangana ndi iwe; ngati iwe ukudziwa poti uyime, dziwa chimene iye amakhulupirira.

¹⁹¹ Chiri monga ngati kutenga mbira ndi kuyimasulira iyo mu khola, ndipo inu kukhala mutatseka una uliwonse. Mungoyima pa chipata; iye ayenera kubwerera mmbuyo. Ndizo zonse ziripo kwa icho. Mwawona? Iye adzayenera kubwerera mmbuyo momwe ku chipata kachiwiri, chifukwa iyo ili njira yokhayo yomwe iye angatulukire. Iye adzakanikizira mutu wake kupyola *apa*, ndipo pafupi kuthyola khosi lake; ndi kupita cha *apo*, cha

apa. Mungoyima ndi kumuyang'ana iye, ndipo iye abwerera mmbuyo momwe. Mwawona? Ndizo zonse.

¹⁹² Ndiyo njira yokhayo yochitira. Khalani nawo Mawu awo. Inu mukhoza kulengeza pozungulira ponse, ndi zikhulupiriro zanu, mungothyola khosi lanu paliponse, koma inu muyenera kubwerera mmbuyo kumeneku Mawu awa. Mwawona? Inde, bwana. Ndizo zonse za Iwo.

¹⁹³ Tsopano, onani, iwo—iwo—iwo—iwo sakuwafuna Iwo. Iwo sakuwafuna Mawu a Mulungu. Chifukwa iye anagwira ku miyambo yake, iye analepheretsa Mawu a Mulungu kuti akhale amphamvu.

¹⁹⁴ Zofanana tsopano, pa Eva wauzimu. Iye sakufuna... Iye akufuna kusunga miyambo yake, ndi kuchoka ku Mawu a Mulungu. Iye akugwira kachiwiri ku zipembedzo, ndi zikhulupiriro zawo ndi miyambo ya akulu ake, mmalo motenga Mawu a Mulungu.

¹⁹⁵ Ndipo pamene lonjezo la Mawu, mu masiku otsiriza, labweretsedwa kwa iye, iye sadzalilandira Ilo, chifukwa, ndi miyambo yake, monga mkwatibwi wa Chihebri anachita. Mawu enieni, ngakhale atawonetseredwa, kutsimikiziridwa, kuvomeredzedwera, iye safuna kukhala nawo Iwo. Chifukwa chiyani iye satero? Chifukwa apo pali choyimira chake. Iye sangakhoze kuchita izo. Ndiko kulondola. Iye sangapose choyimira chake. Mwawona? Ndipo izo zinanenedweratu kuti iye akanadzachita izo, kotero inu mulepheretsa bwanji chirichonse?

¹⁹⁶ Tsopano chinthu chokhacho choti muchite ndicho chabe kukhala wokondwa inu muli mkati. Ndizo zonse. Khalani mukuyembekezera izo. Chabwino.

¹⁹⁷ Mulungu analonjeza, mu masiku otsiriza, kuti Iye akanaawonetsera ndipo akanaatsimikizira Mawu Ake kwa iye, komabe iye sakanachita izo. Zonse zimene, Mulungu anamulonjeza iye, mwa antchito Ake, aneneri. Mulungu analonjeza, kupyolera mwa Yesu Khristu. Mulungu analonjeza, kupyolera mwa Yoweli. Mulungu analonjeza, kupyolera mwa Paulo. Mulungu analonjeza, kupyolera mwa Malaki. Yohane... Mulungu analonjeza, kupyolera mwa Yohane mvumbulutsi, aneneri onse awo, chimodzimodzi basi chimene Uthenga wotsiriza ukanakhala kwa iye. Tsopano, ngati inu mukufuna kuwulemba iwo; ndithudi, inu nonse mukuwadziwa iwo: Yesu, Yohane 14:12; ndi Yoweli, Yoweli 2:38; Paulo, Timoteo Wachiwiri 3; Malaki, mutu wa 4; ndi Yohane mvumbulutsi, Chivumbulutso 10, seventini, wani mpaka seventini. Mukuwona, chimodzimodzi chomwe chikanachitika tsopano! Ndipo, kwa mpingo, ndi chiyani Icho? Mawu mu thupi kupangidwa mnofu pakati pa anthu Ake kachiwiri! Mwawona? Ndipo iwo sakhulupirira konse Izo.

198 Inu mukudziwa zimene Yesu ananena pamene Iye anamuwona Iye...pamene Iye anachita zozizwitsa zija pamaso pawo, ndipo anatsimikizira kuti Iye anali Mulungu? Anatsimikizira kuti, zimene Iye anali kuchita. Iye anali. Iye anali atachita chimodzimodzi. Iye—Iye anati kwa iwo, Iye anati, “O, iwe, Kaperna, amene wadzikweza mpaka kumwamba, ngati zintchito zikanakhala...ntchito zazikulu zikanakhala zitanachitika mu Sodomu, zimene zachitika mwa iwe, iye akanakhala akuyimabe lero.” Ndiko kulondola. Ndipo mu Kaperna, Iye sanachite kalikonse koma kuchiritsa anthu pang’ono, ndipo anawawuza iwo zinsinsi za mmitima yawo, ndipo anatulukamo. A-nha. Ndizo zonse. Mukuwona?

199 Iwo sakudziwa zomwe ntchito zazikulu ziri. Iwo amaganiza izo ziyenera kukhala dongosolo lopambana lalikulu kumene aliyense amayimirira, ndipo woweruza amalankhulapo, ndipo—ndipo mabandi kuyimba, ndi zokongoletsa zikuwuluka, ndipo—ndipo akazi ovekedwa bwino, ndi zawo...ndipo kuyembekezera, ndi onse ama Ph.D, LL.D, ndi chisoti chachikulu, chachitali, ndi makolala otembenuzidwira kumbuyo, ndi zirizonse, iwo onse ayenera kulowamo. “Ndicho chinachake chopambana.”

Mulungu amati, “Ndizo zopusa.”

200 Ndipo Iye amabweretsa kenakake kakang’ono kamene sikamadziwa kusiyana kwa pakati pa mwina ma, ABC, nkomwe, ndi kuchita chinachake chimene chimangoyatsa Mpingo weniweni pamoto. Ndipo ena onse amati, “Gulu la oyera-odzigudubuza.” Mulungu amachitcha *Icho* “chopambana,” ndipo dziko limachitcha *Icho* “chopusa.” Dziko limachitcha *icho* “chopambana,” ndipo Mulungu amachitcha *icho* “chopusa.” Mwawona, mbali iyi ndi iyo basi. Mukuwona? Ndipo chinthu chimene Mulungu wachilonjeza, Mulungu adzachichita ndipo wachichita. Mwawona? Ndi ife pano.

201 Tsopano, komabe, iye akanali monga iye anachitira, Eva wa Chihebri. Iye sakanachita basi icho. Inu mukanakhoza kuwukitsa akufa; inu mukanakhoza kuwona Mzimu wa Mulungu. Yesu anabwera pansu, anadzitsimikizira Iyemwini kuti ali Mwana wa Mulungu. Poyamba, Iye anayamba kulalikirira. Chabwino, iwo anaganiza, “Chabwino, kukhala ngati Munthu wosamvetseka. Ndi ndani Iye, nangabe?” Chabwino, chinthu choyamba inu mukudziwa, anthu kuyamba kunena . . .

202 Zedi, iwo anali atanena, mmbuyo, pamene wotsogolera kubwera Wake anadza, Yohane, iwo anati, “Kodi ndiwe Mesiya?”

203 Iye anati, “Ayi. Koma Iye wayimirira pakati panu penapake.” A-ha. Mukuwona? Chifukwa? Iye ankadziwa, pamene uthenga wake unatenga malo, chimene iye anali woti achite. Iye ankadziwa chimene iye ankadzachichita.

204 Monga ngati Nowa anakhala akumuyang'ana Enoki. Pamene Enoki anapita, Nowa anati, "Kulibwino ndiyandikire ku chombo. Nthawi ili pafupi." Nowa anapitirira kumuyang'ana Enoki. Mwawona?

205 Ndipo Yohane ankayang'anira chizindikiro chimene Yesu anamuwuzwa iye, kapena Mulungu anamuwuzwa iye, kuti aziyang'ana. Iye anati, "Iye akuyimirira pomwe pano tsopano, kwinkwake pakati pa inu. Inu sindikumudziwa Iye, koma ine ndidzamudziwa Iye."

206 Atayimirira pamenepo, iwo anati, "Kodi iwe sindiwe Mesiya?" Anati, "Ife tinatumizidwa kuchokera ku likulu." Aha. Anati, "Akulu, ndi onse, atitumiza ife kuno. Ngati inu muli Mesiya, bwanji inu simukubwera ndi kukazidzindikiritsa nokha kuntunda uko, osati kumusi kuno mu gulu ili la zinthu kumusi kuno! Inu mubwere kuntunda uko ndi kukazidzindikiritsa nokha."

207 Iye anati, "Ine sindine Mesiya." Iye anati, "Ine ndine liwu la mmodzi wofuwula muchipululu."

208 Chimenecho chinapita patali pamwamba pa mitu yawo momwe icho chikanakhoza kupitira. Iwo sanadziwe kanthu za icho, mukuwona, ndipo komabe iwo anali onse akumuyembekezera iye kuti awere. "Koma sakanakhala munthu ngati ameneyo. O, mai, icho chikanadzakhala chowopsya!"

"Ndiwe wochokera ku sukulu yiti?"

"Palibe."

"Kodi iwe uli nacho chikalata chachiyanjano?"

"Ndi chiyani chimenecho?" Mwawona?

209 Iye anali wodzozedwa wa Mulungu. Iye anati, "Pali chinthu chimodzi ine ndiri nacho. Nkhwangwa yayikidwa ku muzu wa mtengo." Tsopano, ndicho chonse iye—ndicho chonse chimene iye anali nacho. Iye ankalankhula mu malankhulidwe a munthu wa kuthengo, osati mwa malankhulidwe a munthu wauzimu; njoka, ndi nkhwangwa, ndi mitengo, ndi zina zotero. Iye—iye sankalankhula mwa malankhulidwe ampingo.

210 Koma Yesu anati sipanakhalepo mneneri wonga iye. "Sipanabadwepo mwamuna mwa mkazi, wonga iye, mpaka tsiku lake." Ndiko kulondola. "Iye anali woposa mneneri." Iye anali mtumiki wa Pangano, anayima pakati pomwe pa—pa nyengo ziwiri, zikubweramo. Mwawona? "Woposa kwambiri mneneri."

211 Ndipo kotero ndiye—ndiye iwo sanamudziwe iye. Iwo sanamumvetse iye. Iye anali ngati munthu wa mtundu wokhala ngati wosamvetseka, kotero iwo sanamusamale iye, mwawona.

212 Ndiye pamene Yesu anabwera, ndiye, ndipo ndithudi sanali oti akamulandire Iye, mwana wa akalipentala uyu, apo panalibe kanthu ngati ako, ali ndi dzina lakuda pambuyo Pake, la “wapathengo.” Ndipo, Iye, iwo sakanapita kukawona munthu ngati ameneyo.

213 Koma, koma penyani chimene Mulungu anachita. Iye anatenga osaphunzira, osawuka, asodzi, anthu akuthengo, alimi, ndi timahule, ndi kuwasiya amaudindo akhale pamenepo. Chifukwa? Chiyani? Chifukwa chiyani Iye anachita zimenezo? Chifukwa chiyani Iye anachita chinthu choterocho? Kodi inu mukanalingalira? Chifukwa chakuti anthu amenewo anamuzindikira Iye kuti ali Mawu. Tsopano tiyeni tingwayang’ana iwo miniti yokha.

214 Apa pali nsodzi mbuli yachikulire, sangakhoze kulemba dzina lake. Baibulo linati iye anali “mbuli ndi wosaphunzira.” Iye akubweretsa nsomba zake ndi kuziyika izo pansi. Akutsikira kumusi uko ndi kukawona chimene chikuchititsa phokoso lonseli. Koma pansi mkati mwa iye, iye ankadziwa kuti Baibulo linanena kuti Mesiya . . . Ahebri onse ankayang’anira Mesiya, chifukwa apo panali kuyenera kukhala chinthu Chamalemba chikuchitika pamene Iye abwera.

215 Panali patakhalala a mesiya ambiri, atawuka ndi kumati, “Ine ndine Iye,” ndipo anawatsogolera iwo kumbali, mwa mazana, ndi—ndipo anawonongeka ndi chirichonse. Koma, onani, uko kunali kusokonezetsa Mmodzi weniweniyo pamene Iye ati abwere.

216 Ife takhalala nazo zofunda za Eliya ndi zikhotho, ndi chinthu china chirichonse, koma uko—ndiko—ndiko—ndiko kusokonezetsa chabe chinthu chenicheni pamene iye ati abwere. Mwawona? Ndiko kulondola. Mitundu yonse ya anthu amene avala miinjiro ndi zovala, ndipo akwiriridwa mu zophimba zamitundu yonse zotembenuzidwa, ndi china chirichonse. Izo siziti . . . Izo—izo zimatsimikizira chabe. Monga dola yabodza, imasonyeza kuti pali imodzi yabwino kwinkawake, ngati inu mutangoyipeza iyo. Mwawona?

217 Kotero apa Iye akubwera. Tsopano olemkezeke awa akutuluka, ndipo iwo anali choncho pa cholowa mmalo chawo! “Chifukwa,” iwo anati, “tsopano, ngati Mesiya abwera, Iye ndithudi abwera kwa Kayafa. Iye adzabwera ku chipembedzo chathu. Iye adzabwera kwa Afarisi.” Asaduki, “Ndizo zomwe inu mukuganiza! Iye adzabwera kwa Asaduki.” Ndi apo iwo anali, onani, chinthu chomwecho iwo ali nacho lero, tsopano.

218 Koma pamene Iye anabwera, icho chinali chodabwitsa. Iye adzabwera, o, zosiyana kwambiri kwa zomwe iwo ankaganiza, koma Iye anabwera molingana ndi Mawu. Ndipo iwo sanali kuwadziwa Mawu.

219 Ndiroleni ine ndinene icho, kwenikweni, kotero inu mudza. . . icho chidzalowerera mpaka pansi. Ine ndikufuna ichi kuti mumvetse icho. Ndilo liri vuto ndi inu lero, onani, inu simukuwadziwa Mawu! Mwawona?

220 Yesu anati, “Inu mukhoza kuzindikira mawonekedwe a mlengalenga, koma zizindikiro za nthawi inu simungakhoze kuzizindikira.”

Anati, “Ife tiri naye Mose.”

221 Kotero, anati, “Ngati inu mukanamudziwa Mose, inu mukanandidziwa Ine.” Sankamudziwa Mose, ndipo chotero iwo sanadziwe. Iwo amangodziwa chikhulupiriro chimene iwo anali atachiswa.

222 Tsopano tiyeni timutenge nsodzi uyu wachikulire. Akuyika dengu lake pansi. Anakankhira ndevu zake zayimvi pansi, ndi kumayenda chotsika, “Ine ndikukhulupirira ine ndimuwone Yemwe uyo ali.”

223 M’bale anati, “Tiyeko. Tiye tipite kumusi uku.” Anati, “Ndi Mnyamata yemwe uja. Ndi Mnyamata ankamunena uja tsiku lina. . . Ine ndinali naye usiku wonse Iye usiku wathawu. Inu mukumudziwa Yohane, yemwe ine ndinali kumunena kwa inu?”

224 “Eya, munthu wakuthengo uja kumusi uko! Eya, ine ndinamva za iye.” “Chabwino,” Simoni wachikulire, inu mukumudziwa, anati, “Ine ndinamva za iye kumusi uko. Eya, anali kumusi kumeneko, miyezi iwiri kapena itatu yapitayo, kumusi uko. Inde.”

225 “Chabwino, iye anati. . . Ndipo tsiku limodzi iye anali kuyimirira kumeneko, iye ananena chinthu chosamvetseka. Iye anati, ‘Inu mukudziwa, apa Iye akubwera pakali pano!’ Iwo anati, ‘Iwe ukudziwa bwanji?’ Anayang’ana cha kumeneko; Munthu wamba chabe atayimirira pamenepo. Iye anati, ‘Ine ndikuwona Mzimu wa Mulungu, monga nkhunda, ukubwera pansi. Ine ndikumva Liwu likulankhula, ‘Uyu ali Iye. Uyu ali Mwana Wanga wokonedwa mwa Yemwe Ine ndikondwera kukhalamo.’” Ndiye iye anayenda mumadzi momwe ndipo anamubatiza Iye, zina zotero. Chabwino, pamenepo, iye anati iye anamudziwa Iye.”

226 “O, ine sindikudziwa,” Simoni anati. “Ine ndinamva zonse za izo, nthawi zambiri.” Koma apa iye akudzapo. Koma pansi mu mtima wake munali mbewu yokonzedweratu. Mwawona? Yesu ananena choncho. Kulondola. Akuyenda mpaka kwa Iye. Akuyenda kupita. Anati, “Ine ndipita ku msonkhano komweko ndikawone.” A kuyenda kupita kumeneko.

227 Yesu anali kuyimirira pamenepo, Kamunthu wamba chabe kakang’ono. Anayenda kupita. Iye anati, “Bwanji, dzina lako ndiwe Simoni. Ndipo dzina la abambo ako linali Yonasi.” Izo

zinamuphwesa iye. Chifukwa? Kakang'ono ako, kambewu ka Moyo Wamuyaya kanakhudzidwa mkati umo. Inde, bwana.

228 Anati, “Dikirani miniti! Ziri bwanji choncho? Inu simunandiwonepo ine. Ngakhalenso kuti inu mukuwadziwa abambo anga, chifukwa iwo anali atamwalira kwa zaka. Koma apa Inu mwabwera, kundiwuza ine zimenezo? Tsopano, ine ndikudziwa kuti Baibulo limati...” Tsopano, ndicho osati kubwerera ku zimene akulu amanena. “Koma Baibulo linanena kuti Mesiya akanadzakhala mneneri. Apo Iye ali. Ndiye Iye.”

229 Tsiku limodzi Iye anadutsa kupyola Samaria, akupita mmusi kupyola pamenepo ndi gulu la Ayuda. Iye anawasiya iwo. Ndipo wamng'ono uyu, mkazi wa mbiri yoipa anatulukira, mwinamwake dona wamng'ono wokongola, inu mukudziwa. Ndipo iye anali atapotozedwera pa msewu, ali mwana. Ndipo iye anali kupita kupyola kumeneko. Mwinamwake iye anali kuganiza za chinachake. Iye anayenda mpaka kumeneko ndi kuyika chidebe pansi. Ndipo iye anayamba kuponyera chotungira pansi, inu mukudziwa, kutunga madzi. Ndipo iye anamva Mwamuna akuti, “Ndibweretsere Ine akumwa.” Iye anayang'ana pozungulira, ndipo apo panakhala ngati Myuda wa zaka zapakati.

230 Iye anati, “Mnena, kodi Inu sindinu Myuda? Inu musamachite zimenezo. Sindiwo mwambo wake kuti Inu mulankhule kwa ine. Ine ndine Msamariya.”

231 Iye anati, “Koma ngati iwe ukudziwa Yemwe iwe ukulankhula naye, iwe ukanabweretsa... iwe ukadandifunsa Ine kuti ndikupatse iwe akumwa.”

232 Anati, “Chidebe Chanu chiri kuti?” Mwawona? “Chingwe Chanu chiri kuti?”

“Chabwino,” Iye anati, “madzi amene Ine ndimapereka ali Moyo.”

233 “Chiyani?” Mwawona? “Bwanji,” iye anati, “bwanji, inu nonse mukufuna kupembedza mu Yerusalemu. Ndipo makolo athu ankapembedza...”

234 “O,” Iye anati, “uko nkulondola, koma,” anati, “ife Ayuda timadziwa chimene ife tikupembedza. Koma,” anati, “inu mukudziwa, nthawi ikubwera pamene—pamene anthu sadzapembedza mu Yerusalemu kapena mu phiri ili.” Iye anati, “Iwo ali—iwo adzapembedza Mulungu mu Mzimu, chifukwa Iye ali Mzimu, Mzimu ndi Choonadi.” Chabwino, iye anayamba kuwerenga, inu mukudziwa.

Ndipo Iye anati, “Pita ukatenge mwamuna wako ndipo ubwere kuno.”

Iye anati, “Mwamuna wanga? Ine ndiribe mwamuna aliyense.”

235 “Bwanji,” anati, “ndicho choonadi.” Anati, anati, “Iwe wakhala ukuthamanga nawo asanu, ndipo uli naye wachisanu ndi chimodzi tsopano.” Ndipo anati, “Iwe wakhala nawo asanu. Ndipo—ndipo, iwe, iwe ukudziwa. Iwe wanena zowona.”

236 Yang’anani! Chinali chiyani icho? Kuwala uko kunakhudza mbewu imeneyo. Iyo inali itagona mmenemo, imene inalankhulidwa ndi Mulungu. Inde, bwana.

237 Mbewu inali padziko lapansi. Pamene Mulungu anasunthira madzi kumbali, ndi dzuwa linayigunda iyo, iyo inatulukira. Ndiko kulondola. Mwawona? Ndizo zonse chimene iyo inkasowa, linali dzuwa. Inkasowa kuwala kokha. Inde, bwana.

238 Ndiyeno pamene Mzimu Woyera, mwa Iye, unasuntha moyo wake wakale, ndipo kunachiwonetsa icho kwa iye, Kuwala kumeneko kunakhudza iyo. Iye anati, “Bwana, ine ndazindikira Inu ndinu Mneneri.” Iye anati, “Tsopano, ife tikudziwa, ine ndikudziwa izo, kuti pamene Mesiya abwera, ndicho chimene Iye ati adzakhale. Ndipo ife sitinakhale naye mneneri kwa zaka mazana. Ife sitinakhalepo naye mneneri wowona, kwa zaka mazana.” Ndipo iye anati, “Inu mukundiwuzwa bwanji ine za mwamuna wanga, ndipo mwandiwuzwa ine angati amene ine ndakhala nawo, ndi zina zotero. Bwanji,” anati, “Ine sindikumvetsa izi.” Anati, “Pamene Mesiya abwera, chabwino, Iye adzachita zimenezo. Koma Inu ndinu Yani?”

Iye anati, “Ine ndine Iye.”

Chinali chimenecho. Mwawona? Kahule!

239 Ndipo ansembe anayang’ana pamenepo ndipo anati... Chabwino, iwo ayenera kukayankha kwa gulu lawo. Anati, “Musati wupusidwe naye Munthu ameneyo. Iye ali—Iye ali wodzazidwa naye mdiererekezi. Ndizo zonse.” Tsopano, ndicho kusiyana kwake. Ndicho chinthu chomwecho lero. Mwawona? Chinthu chomwecho lero, chikugunda chimodzimodzi basi. Eya. Inde, bwana.

240 Iye, iye anadziwa icho, chifukwa Kuwala kunayikhudza Iyo. Iwo a-. . . Iwo asodzi, anthu akuthengo, alimi, osonkhetsa msonkho, timahule, iwo anawona mwa Iye chimene Malemba ophweka anati Iye akanadzachita. Ndipo Afarisi sakanakhoza kuwona, chifukwa cha miyambo yawo. [M’bale Branham ayimikira ndi kuchita mwanjira yina. Osonkhana avomereza motsimikizira—Mkonzi.] Iwo sakanakhoza kuwona, chifukwa miyambo yawo. Koma wachiwerewere, alimi, ndi iwo onse, iwo anachiwona Icho, onse amene anali okonzedweratu. Pamene kukayikira kunakungunuka, mbewu inapita kukamera. Ndiko kulondola.

241 Kodi anachita chiyani iye? Iye anati, “Chabwino, ine ndiri wokondwa ndinakumana naye Mesiya”? O, ayi, m’bale. Mpaka mu mzinda iye anapita. Iye anayiwala za madzi. Iye anati, “Bwerani, mumuwone Munthu Yemwe wandiwuzwa ine zinthu

zomwe ine ndazichita. Kodi ichi sichiri chinthu chomwecho chimene Lemba limati Mesiya adzachichita? Kodi ichi sichiri chimodzimodzi chimenecho?” Ndipo anthu akanakhoza kuwona chinthu chomwecho.

²⁴² Monga Yesu Khristu anati, mu Yohane Woyera 14:12, izo zikanachitika kachiwiri. Iye ananena ichonso mu Luka, pamene Iye anati, “Monga izo zinaliri mu masiku a Nowa.” Momwe Mulungu anadziwonetsera Yekha mwa Munthu, ndipo anamuwuzwa yemwe anali kuseri kwa Iye; ndi chimene Sarah anachita, kuseka mu hema. Ndipo Malemba onse awa, a Malaki, ndi ena otero, ananeneratu mu masiku otsiriza. Ahebri 4 anati, pamene “Mawu” abwereranso. Malaki 4 anati Iwo akanabwereranso ndi munthu. Ahebri 4 anati, “Mawu a Mulungu amazindikira maganizo amene ali mu mtima.”

²⁴³ Ndipo iwo akhoza kuwona icho chikuchitika, ndi kuchokapo kwa icho. Miyambo yawo yabisa icho ndi kuchipanga icho chopanda mphamvu. Chabwino, ife tiri chabe apa. Ndizo zonse. A-nha.

²⁴⁴ Inu mukudziwa, Iye akanakhoza kuchita chinthu chomwecho lero. Iye akhoza kubwera powonekera pomwe ndi kuwonetsa zinthu zomwezo Iye anzichita apo, monga Iye anati Iye akanachita. Mwawona? Iye analonjeza kuchita izo. Iye analonjeza kuchita izo. Ndipo ngati Iye akanachita chinthu chomwecho, mtumiki wa Laodikaya akuyenera kuti achite izo.

²⁴⁵ Ndiyeno ngati mpingo wa Laodikaya ukuwona izo zikuchitika, iwo adzachita chimodzimodzi basi monga mpingo wa Chihebri unachitira pachiyambi. Ziribe kanthu kaya Iwo ali otsimikiziridwa mwabwino chotani, o, iwo akanachita izo, basibe. O, mai!

²⁴⁶ Tsopano, Iwo amanena kuti iwo akanatero. Ife tikanabwerera ku Mawu apachiyambi, ndi kuwonetseredwa monga kunalonjezedwa, kubwezeretsa kachiwiri Chikhulupiro, Chikhulupiro chapachiyambi, kachiwiri. Ndipo ngati Iye anadzindikiritisa Yekha kuti Iye anali kukhala pakati pa anthu Ake, pa kuchita zinthu izi; Iye akanakhoza ngakhale kutoletsa chithunzi Chake, mwasayansi kutsimikizira izo. Ndipo komabe iwo sakukhulupirira izo. Ndi kutsimikiziridwa, kulola diso la makina a kamera kumugwira Iye atayimirira pamenepo, Lawi la Moto lomwelo, yemweyo dzulo, lero, ndi nthawizonse, Ahebri 13:8 kusonyeza kuti izi—ziri mwasayansi, ndi njira ina iliyonse, mwasayansi mu malo auzimu. Mwa njira iliyonse izo zikanakhoza kutsimikiziridwa, izo zatsimikiziridwa.

²⁴⁷ Ndipo, inu mukudziwa, iwo mwinamwake akanachita chinthu chomwecho. Iwo mwinamwake akanangoyenda nthawi yomweyo ndi kuchita chinthu chomwecho monga iwo anachita.

248 O, Mulungu, tithandizeni ife! O! Ife tingoyimira apa. Koma, Mulungu tithandizeni ife kuti tipenye tsopano, pemphero langa, pamene ife tikubwera tsopano. Chifukwa, ine sindikufuna kukusungani inu mochedwa kwambiri. Mulungu tithandizeni ife kuti tipenye. Ine ndikukhulupirira mwinamwake, Mzimu pa ife, iwo ukanakhala pakali pano kuti Iye akanatithandiza ife kuwulula, kuchitsegula Chisindikizo ichi.

249 Tiyeni tiwerenge. Pamene ife tikuwona chikhalidwe chimene mpingo ulimo, ife tikuwona pamene iwo wakhala uli, tinawona zimene iwo anachita, tinawona pamene iwo unkeyenera kuti ufiye, kuziwona izo apo, ndi kuwona zomwe iwo ankeyenera kuti achite. Iwo anachita izo basi. Tsopano inu mukuwona pamene ife tiri? Inu muzichita kuweruzako. Ine sindingakhoze kuweruza. Ine ndiri nawo chabe udindo wobweretsa Mawu awa. Basi monga Iwo aperekedwera kwa ine, ine ndikhoza kuwapereka Iwo. Mpaka Iwo ataperekedwa kwa ine, ine sindingakhoze kuwapereka Iwo; palibe mmodzi aliyense angakhoze.

Ndipo pamene iye anatsegula chisindikizo chachitatu, ine ndinamva chamoyo chachitatu chikuti, Bwera ndipo udzawone. Ndipo ine ndinapenya, ndipo taonani kavalo wakuda; ndipo iye amene anakhala pa iye anali nayo miyeso iwiri mu dzanja lake.

Ndipo ine ndinamva liwu pakati pa zamoyo zinai likuti, Muyeso wa tirigu wogula rupiya, ndi miyeso itatu ya barele yogula rupiya; koma penya iwe usawononge mafuta ndi. . . vinyo.

250 Tsopano, Mwanawankhosa ali nalo Bukhu mu dzanja Lake, akumatula Zisindikizo. Iye wamatula chimodzi choyamba, chimodzi chachiwiri, ndipo tsopano Iye akumatula chimodzi chachitatu. Ndipo pamene Iye akumatula icho, Mwanawankhosa akumatula icho, Chisindikizo Chachitatu, Chamoyo chachitatu. . .

251 Tsopano ndi angati akudziwa chimene Chamoyo chachitatu chinkawoneka ngati? Chinkawoneka ngati munthu. Chimodzi choyamba chinkawoneka ngati mkango; chimodzi chinacho chinkawoneka ngati mwanawang'ombe, kapena ng'ombe; ndipo chimodzi chachitatu chinkawoneka ngati munthu, monga munthu. Ndipo iye anamva—Eholengedwa Chamoyo, c—Chirombo. Cholengedwa Chamoyo, chonga munthu, chinati kwa Yohane, “Bwera, udzawone chimene Icho chiri, chinsinsi ichi chimene chakhala chobisika.” Monse mmusi kupyola mu zaka za chiwombolo, chikhazikitsireni maziko a dziko, Icho chakhala chobisika pansu pa Chisindikizo ichi, zomwe ziti zichitike. Tsopano, “Bwera, yang'ana chimene Icho chiri.”

252 Ndipo koteru Iye akuchitsegula Icho. Bingu likuphulika, ndipo Mwanawankhosa akutsegula Zisindikizo.

253 Tsopano, ndipo Yohane anayenda kubwera apo, kuti akawone chimene Icho chikanati chikhale. Kodi iye anawona chiyani? Iye anawona kavalo wakuda. Ndipo wokwera wake anali nayo miyeso, kapena milingo, mu dzanja lake. Tsopano, ndicho chinthu choyamba iye anawona. Pamene Mwanawankhosa analengeza Icho, amatula Chisindikizo, ndiye Chamoyo china... Onani, Zamoyo izo zikupatsana nthawi, ya kulengeza, “Bwera, udzawone.” Ndipo Yohane, pamene iye anali kuyimirira, mwinamwake monga *chonchi*, iye akuyenda mpaka apa, pamene Mwanawankhosa anatsegula, ndipo anapita patsogolo. Kawirikawiri. . .

254 Bingu likugunda, monga ife tinawona Chisindikizo Choyamba. Ndipo iye akuyang’ana kuti awone chimene chiti chichitike. Ndipo iye akuwona munthu akubwera, poyamba, pa kavalo woyera. Iye akumuyang’ana iye atakwera akupita. Ndipo mpaka mmusi kupyola, Yohane akumuwona iye mpaka ku mapeto. Iye akumuwona iye akubwera mmusi, kavalo woyera wake, ali nawo uta mu dzanja lake, ndipo—wokwerayo ali nawo, ndipo iye alibe mivi nawo iwo. Ndipo chinthu chotsatira chimene iye akuchiwona, iye akutenga korona, akukwera pomwepo kupyola.

255 Ndiye ife tikupeza, ndiye, Mwanawankhosa, apa iye akubwera kachiwiri, Iye akutsegula chimodzi china. Ndipo akuyang’ana. Tsopano apa pakubwera k—kavalo wofiira. Munthu uyu ali nalo lupanga mu dzanja lake. Iye akukwerabe mpaka mmusi kupyola Lemba, onani, ndi lupanga ili mu dzanja lake, ndipo anali woti akaphe ndi kuchotsa mtendere pa dziko lapansi.

256 Tsopano Mwanawankhosa akutsegula Chisindikizo china. Mmodzi wina wa Zolengedwa zamoyo, chonga munthu, chinati, “Bwera, udzawone.” Tsopano iye akuyenda kupita, kukawona chimene ichi chiri. Ndipo pamene iye akutero, apo akubwera wokwera pa kavalo wakuda.

257 Tsopano, usiku watha, ife tinapeza kuti wokwera yemweyo amene anakwera kavalo woyera anali mmodzi yemweyo pa wofiira uyo.

258 Ndipo Liwu linati, mkati mwa Zamoyo, linayitana uko, inu mukuwona. Apo, kubwera kuti awone chimene icho chinali: Iye anali mu Zolengedwa zamoyo izi. Ndipo iye anawona kavalo wakuda uyu.

Ndipo pamene... liwu mkati mwa zamoyo zinai linayitana uko, Muyeso wa tirigu wogula rupiya, ndi—ndi miyeso itatu ya barele yogula rupiya; koma ona kuti iwe usawononge ayi m—mafuta ndi vinyo. (Mwawona?)

259 Wokwera uyu, tiyeni tikambirane za iye. Ngati inu muti muzindikire wokwera woyamba, amene iye anali. Ndipo ife tinapezapo, usiku watha, Mwamalemba, kuti wokwera

wachiwiri anali chimodzimidzi munthu yemweyo, kokha kuti iye anali pa kavalo wina. Chinachitika nchiyani? Iye anasintha utumiki wake. Mwawona? Kulondola. Ife tinapeza iye anali wotsutsakhristu, ndipo iye anali atasintha malo ake.

²⁶⁰ Ife tinapeza kuti pamene iye, poyamba, anali chabe kavalo woyera, iye anadzakhala chiphunzitso. Tsopano, ife tatenga chirichonse cha izi mobwerera kumene mu Malemba. Mwawona?

²⁶¹ Tsopano, yang'anani pamene ife tiri, usiku uno, m'badwo wa mpingo wina uja tsopano. Mwawona? Ife tikubwera mpaka ku m'badwo wa mpingo wachitatu tsopano. Mwawona? Chimodzimidzi basi pa m'badwo wa mpingo wachitatu, ziri basi chimodzimidzi monga kavalo wachitatu. Mwawona?

²⁶² Tsopano, m'badwo wa mpingo woyamba, iwo unali chiyani? Achinikolai anali nacho chiphunzitso, onani, chimodzi choyamba chokha. Chabwino. Ndiyeno, chinthu choyamba ife tikudziwa, chiphunzitso cha Chinikolai ichi, icho chikufika pololezedwa ndipo chinali cholondola, chinayamba kuchitapo kanthu. Ndipo iwo anamuveka korona munthu uyu. Ndiye, mzimu uwu, wotsutsakhristu, ukukhala mu thupi mwa munthu. Mwawona? Ndipo ife tikupeza, kenako, iye akukhala Mdierekezi mu thupi, nayenso; chiwanda chikuchoka, ndipo Mdierekezi akudzalowamo.

²⁶³ Ndipo monga momwe mpingo uwo uli wa mtundu umenewo, mpingo wotsutsakhristu, ukupambana; kotero ayenera Mkwatibwi kubwera motsatana nazo zinthu zosiyana: kupyola kulungamitsidwa, kuyeretsedwa, ubatizo wa Mzimu Woyera, ndi kumasuntha chopitirirabe, onani, basi monga choncho. Kokha, iwo atenga chitsitsimutso chawo poyamba, ndipo Mpingo ukutenga icho potsiriza. Zaka zawo zitatu zoyambirira... masiteji atatu oyambirira a iwo amene anapyola m'badwo wa mdima; ndiye yachitatu, masiteji atatu, ukutuluka Mpingo; kuchokera ku kulungamitsidwa, kuyeretsedwa, ubatizo wa Mzimu Woyera, kukhala mwa thupi Mulungu kuwonetseredwa pakati pathu. Apa iye akubwera mkati, monga wosutsakhristu, monga mneneri wabodza, ndiye chirombo, ndiye mu m'badwo wa mdima. Ndipo Mpingo ukubwera kuchokera mu m'badwo wa mdima uwo; kulungamitsidwa, kuyeretsedwa, ubatizo wa Mzimu Woyera, Mawu mu thupi, njirayo tsopano. Ndipo iye akupita mmusi. A-ha. Inu mukuwona zimenezo? Iye akupita pansu. Mpingo ukupita mmwamba. Mwawona? Izo ziri basi mwangwiro monga izo zingakhalire. O, ndi zokongola. Ine ndikungozikonda izo.

²⁶⁴ Wokwera uyu ali mmodzi yemweyo, koma siteji yina ya utumiki wake.

265 Siteji yoyamba, kavalo woyera, onani, iye anali mphunzitsi chabe, mphunzitsi chabe wotsutsakhristu. Iye anali kutsutsa Mawu a Mulungu.

266 Ndipo tsopano inu mungakhale bwanji wotsutsakhristu? Aliyense amene akana kuti Mawu alionse a izi sali owona, ndi kuti akhale akuphunzitsidwa basi mofanana, ali wotsutsakhristu, chifukwa iwo akukana m—m—m—Mawu. Ndipo Iye ali Mawu.

267 Tsopano, siteji yoyamba, kavalo woyera, iye anali chabe mphunzitsi, koma mzimu wotsutsakhristu mu chiphunzitso chake ndi mawonekedwe ake. Iye anali wosalakwa. Iye sakanakhoza kupweteka kanthu, ankawoneka ngati; akupitirira be choncho. Ndiyo njira yomwe Satana amalowera mkati. O, iye ali mbalame yothyathalika.

268 Iye anamuwuzwa Eva, anati, “Tsopano, iwe ukudziwa iwe ukufunafuna nzeru. Iwe sukudziwa chimene chiri chabwino ndi cholakwika.” Anati, “Tsopano, ngati maso ako akanatseguka, iwe ukanadziwa chomwe chiri.” Ndipo anati, “Chipatso chiri chosangalatsa. Ndi chabwino. Ndi—ndi chosangalatsa kwa diso. Iwe uyenera kudya icho tsopano. Iwe sukudziwa kaya icho chiri, kapena ayi, kodi iwe?”

“Ayi, ine sindikutero. Koma Mulungu anati ndisachite icho.”

“Koma, o, chabwino, ine ndikudziwa, koma . . .”

“Mulungu anati Iye . . . ife tikanafa.”

269 Iye anati, “Ndithudi Iye sangachite zimenezo.” Onani, mokoma basi momwe izo zingakhoze kukhalira. Taonani chimene icho chinachita.

270 Uyang’aneni mzimu wotsutsakhristu uwu ukuwuka pakati pa mpingo woyambirira, chiphunzitso cha Chinikolai. *Nikao*, “kugonjetsa” anthu wamba, kupanga munthu woyera. O, icho chiri monga ngati chos- . . . “Chabwino, ife tikungofuna chiyanjano. Bwanji, inu mwamwazikana kunja kuno; palibe amene akudziwa kumene wina ali. Ine ndikuganiza ife tonse tiyenera kukhala nalo bungwe ndi kukhala osiyana basi. Onani, ife tipite, kukaziyika tokha palimodzi. Ife tiyenera kupanga mphanga yake.” Ndipo ndicho chimene icho chiri. Palibe chinthu choterocho monga Mpingo wa Chikhristu wa Methodisti. Umenewo si Mpingo; imeneyo ndi mphanga. Baptisti, umenewo si Mpingo; ndiyo mphanga.

271 Pali Mpingo umodzi wokha, ndipo ndiwo Thupi lachinsinsi la Yesu Khristu. Ndipo inu mumabadwira Mmenemo, ndiko kulondola, mwa kukonzedweratu. Ndiko kulondola. “Zonse zimene Atate andipatsa Ine zidzabwera. Palibe munthu angakhoze kubwera pokha Atate atamuyitana iye. Ndipo onse amene Iye andipatsa Ine, adzabwera kwa Ine.” Koteru, izo, ndizo izo. Iye basi . . .

272 Mwanawankhosa akukhala pamenepo, akupanga—akupanga chitetezero, mpaka mmodzi wotsiriza atalowa mkati. Mabelu ang’ono akuyimba, ndipo Iye akutuluka ndi kutenga cholowa Chake ndiye, onani, ndicho chonse; akuwubweretsa Mpingo Wake Kwawo, omumvera Ake. Ndi kuponyera mdani Wake mu Nyanja ya Moto, ndi onse a omumvera ake kulowa mmenemo ndi iye, ndipo ndi zimenezo. Ndiye ife tikuyenda kumka mu Zakachikwi.

273 Wokwera yemweyo, tsopano. Siteji yoyamba iyi, iye anali wosalakwa. Ndipo yachiwiri, tsopano, ngati inu munapita mmwamba pang’ono, kuposerako pang’ono apo; siteji yachiwiri, Baibulo linati iye “akanadzapatsidwa korona.” Ndipo iwo anamuveka korona munthu, munthu wapamwamba. Onani, kumuveka korona iye! Ndipo, ndiye, Baibulo silinamutche iye papa. Baibulo linamutcha iye “mneneri wabodza.” Chifukwa? Eya. Zedi, iye ayenera kukhala mneneri wabodza, mwa mzimu wotsutsakhristu wake, umene unkaphunzitsa kutsutsakhristu motsutsa Mawu apachiyambi. Chifukwa, ngati iye ankaphunzitsa motsutsa Mawu apachiyambi, chinali chotsutsakhristu. Icho chinali. Ndipo Mawu ali Mulungu, onani, Khristu. Chabwino. Tsopano, zitatha izo, ife tikumupeza iye ndiye atavekedwa korona. Ndipo pamene iye anavekedwa korona, tsopano, iye ali wosalakwa kwambiri ndi wopanda chomuthandiza. Iye ali chabe kamunthu kakang’ono.

274 Koma ndiye mu Bungwe laku Nicaea, iye anapangidwa chimenecho, ndipo Konstantini anamupatsa iye chuma chonse. Ndiyeno kodi anachita chiyani iye? Ndiye iye, onani, Satana, anamupatsa iye mpandowachifumu wake ndi ulamuliro. Baibulo linanena choncho, monga ife tapyola zimenezo.

275 Tsopano, chinthu chotsatira ife tikuchipeza, kuti Mdierekezi akulamulira ndale zonse zimene zakhala ziripo kapena ziti zidzakhalepo konse. Ife tinapeza izo mu Mateyu 4:11. Ndipo ife tsopano tikupeza, ndiye, kuti Satana anali nazo kale ndale.

276 Koma iye akuyesera kuwutenga Mpingo, kotero iye akupita mmusi kuti akawunyenge Iwo. Iye akutenga munthu wake wapamwamba, akumugwiritsa ntchito iye mu bungwe, ndi kumuveka iye korona “vicar,” mwawona, khristu. Khristu anachita mmalo mwa Mulungu. Onani, munthu uyu ali vicar, mmalo mwa Mulungu. Mwawona? zofanana basi, “mmalo mwa Mulungu,” chomwe iye akuyenera kuti akhale, vicar pansu pa Khristu.

277 Tsopano, tsopano, pamene iye anachita izo, ndiye iye anachita chiyani pamenepo? Iye, Satana, anatenga mphamvu yake yandale, imene iye anali kale pamwamba pake, ndipo anatenga mphamvu ya zipembedzo, imene iye anali kale atavekedwa korona, ndi kuziyika izo palimodzi.

278 Ndiyeno iye anamupangira iye korona wina waku gehena. Ndi iwo amene anali atamwalira, ngati iwo akanadzalipira ndalama zokwanira, iye akanadzawatulutsa iwo. Mwawona? Kotero tsopano iye ali—iye ali vicar wa Kumwamba, wa ku purigatorio, monga iye akufunira kuchitcha icho. Mulibe chinthu choterocho mu Baibulo, onani, koma iye anayenera kupanga chinachake. Baibulo linati icho chinachokera ku phompho lopanda malire, ndi kubwereranso mmbuyo njira yomweyo. Ndipo, pa dziko lapansi, wolamulira!

279 Tsopano kodi iye anapatsidwa chiyani ndiye? Poyamba, iye anali nawo uta, koma anali alibe muvi uliwonse. Koma tsopano iye ali nalo lupanga lamphamvu mu dzanja lake. Iye akhoza kuchita chinachake tsopano. Ndiye iye akulumphaka kuchoka pa kavalo wake woyera; kavalo woyera akupitabe kunja. Tsopano iye akukwera chiyani? Kavalo wofiira, magazi, kavalo wa kufiira kwa magazi. Iye kwenikweni akukwera mmodzi ameneyo. O, zedi. Tsopano iye wapatsidwa mphamvu yayikulu ndi lupanga lamphamvu, kuti aphe, ndiye iye akukwera kavalo wake wofiira mwamagazi.

280 Ife tikuwona, kuchokera ku Chisindikizo Chachiwiri, chimene chinamatulidwa usiku watha, iye anali atatenga mtendere kuchoka padziko lapansi ndipo anaphana wina ndi mzake. Ndipo mbiriyakale ya ofera yake yomwe, ya mpingo Roma Katolika, imawonetsa kuti iwo anayika a Chiprotestanti mamilioni makumi asanu ndi amodzi mphambu asanu ndi atatu ku imfa, kuchokera nthawi ya Hippo Woyera waku... kuchokera pa Ogasitini Woyera waku Hippo, mpaka 1580 chinachake. “Mamilioni makumi asanu ndi amodzi mphambu asanu ndi atatu.” *Great Reform* la Schmucker, ngati inu mukufuna kuwerenga zimenezo, *Glorious Reform*, kani, mwawona. Tsopano, mamilioni makumi asanu ndi amodzi mphambu asanu ndi atatu olembedwa pa mbiriyakale ya ofera! Pamene mmodzi wa wotchedwa woyera wawo anapeza vumbulutso lakuti aliyense amene sagwirizana nawo mpingo waku Roma ayenera kufa monga wosokoneza, chimenecho chinawakhazika chabe iwo mozungulira apo. Mnyamata, iye anapita kukakhetsa magazi! Iye—iye analumphaka pa kavalo woyera wake... pa kavalo wofiira wake, ndipo iye anapita akukwera. O!

281 Tsopano mphamvu yake yopambana ikubwera. Iye anapangidwa vicar wa Kumwamba, ndi kumapembedzedwa ngati Mulungu. Wolamulira wa dziko lapansi, pa kulumikizanita mpingo ndi dziko palimodzi, kumupanga iye wolamulira pa dziko lapansi; kumupatsa iye korona pa icho. Iye akhoza kupempherera miyoyo kuchoka ku purigatorio. Iye akhoza nayenso kutete... Iye anali monga ngati Mulungu, pa dziko lapansi, mmalo mwa Mulungu. Palimodzi, iye anali nayo mphamvu yaikulu kuti aphe aliyense amene sanagwirizane

ndi kulamulira kwache. Ndani ati alankhule chirichonse kwa iye? Mpingo sungalankhule kanthu; iye ali mutu wa iwo. Dziko silingalankhule kanthu; iye ali mutu wa ilo. Kotero, iwo anafa mwa mamilioni. Yonse mipingo iyo yaying'ono, m'bale, inaswedwa, ndi kuphedwa ndi kukanthidwa, ndi kudyetsedwa kwa mikango, ndi china chirichonse. Mukuwona? “Chinjoka,” Roma, “anamupatsa iye mpando wake ndi ulamuliro.” Baibulo linanena choncho. Mukuwona? Kotero iye anakwera wofanizidwa wake, kavalo wofiira kupyola mu magazi a anthu, mpaka iye anadzakhala kavalo wofiira.

²⁸² Tsopano Yohane akumuwona iye pa kavalo wakuda. Iye anasintha, chinachake.

²⁸³ Tsopano ine ndiyenera ku—kulankhula ichi basi momwe chabwerera kwa ine. Ndiyeno ndipo ngati icho chibwera kwa ine ndipo nkusafanana nawo Malemba enaonse, ndiye Mulungu sanandipatse icho. Mwawona, Malemba ayenera kutero, aliwonse a iwo, iwo ali chabe chinthu chimodzi chachikulu—chinthu chachikulu ngati chimenecho. Lemba liyenera kugwirizana nalo Lemba. Ndipo chirichonse chiri chosiyana kwa Lemba . . . Ngati Mngelo ameneyo wa Ambuye akanandiwuza ine chirichonse chimene sichinali cha Mwamalemba, ine sikanamukhulupirira Iye.

²⁸⁴ Ine ndinati, uko mu Chicago tsiku lina, pamene iwo onse mazana a azitumiki . . . Kodi analipo wina pa msonkhano umenewo? Ndithudi. Msonkhano uja mu Chicago, ine ndinati, “Tsopano, inu nonse mumanena zakuti muli ndi . . . Inu mumaganiza inu munali kundipiringiza ine mkati apa, pa chinachake.” Pafupi monga mmene uliri mu chipinda chino tsopano. Ine ndinati, “Nchiyani chimenecho? Inu muli nacho icho monditsutsa ine.” Ine ndinati, “Mzimu Woyera unandiwonetsa ine, mausiku atatu apitawo, pamene aliyense wa inu akanadzakhala. Ndipo ife sitikanadzakhalamo mmenemo . . . Mumfuse Carl apa ngati izo siziri zolondola.”

²⁸⁵ Ndipo panali Hank ndi onse a iwo, “Ndiko kulondola.” Inu nonse munali pamenepo kukamvera.

²⁸⁶ Ine ndinati, “Tsopano inu muli nacho kuti munditsutse ine, pa Kuphunzitsa kwanga. Ndilo lomwe liri vuto. Tsopano ine ndikufuna mmodzi wa inu abwere apa, ndipo tengani Baibulo lanu ndi kuyima pafupi ndi ine, ndi kuchitsutsa Icho.” Ilo linali gulu la chete kwambiri limene inu munalimvapo. Ine ndinati, “Chavuta nchiyani ndi inu?” Ine ndinati, “Ndiye, ngati inu mukudziwa kuti inu simungakhoze kuyima kutsutsana nawo Mawu, ndiye chokani kumbuyo kwanga. Inu Madokotala Auzimu ndi chirichonse, ndi kumalankhula momwe, kudzidziwitsa nokha monga ‘Dokotala,’ ‘Dokotala,’ ‘Dokotala,’ Ndipo ine ndine . . .” (O, M'bale Woods ndi ine tinati “cheekchaker,” kapena, “greenhorn.”) “Ine ndiribe maphunziro,

sindinabwere kupyolera mu seminare iliyonse kapena sukulu. Koma inu mutenge Baibulo lanu ndi kubwera apa ndi kuyima pambali panga, tsutsani mbewu ya serpenti, ubatizo mu Dzina la Yesu, kapena chirichonse cha zinthu izo zimene ine ndimaphunzitsa.” Palibe aliyense ananena liwu. Inu nonse mukudziwa zimenezo. Ilo linali gulu lachete kwambiri limene inu munaliwonapo konse.

²⁸⁷ Onani, iwo amangokuwa ngati ine sindikudziwira chiyani. Tsopano, tsopano apa izo ziri. Ine sindimakhulupirira mu kukangana nawo anthu, koma pamene zifika pamalo amene iwo ayesera kukukokera iwe mu icho. Ndipo ine sindikanapita, koma Mzimu Woyera unandiwuza ine, unati, “Pita mpaka kumeneko. Ine ndikayima pambali pako.”

²⁸⁸ Ndinawawuza iwo, masiku atatu kapena anayi isanafike nthawi. Inu nonse munali kumeneko ndipo munawamva Bambo Carlson ndi iwo, ndi—ndi Tommy Hicks. Ndi onse a iwo atakhala pamenepo. Ndipo ine ndinapita, masiku atatu zisanachitike, ndipo ine ndinati, “Inu mukasintha malo amenewo.”

²⁸⁹ Iwo unali usiku wa mkuntho. Ine ndinali ndi msonkhano. Iye anati, “Pita, ukayime pa zenera lija, pa chitseko chaching’ono chachitatu chija kumeneko.” Ndipo ine ndinapita kumeneko ndikukayima mkati momwemo. Ine ndinayang’ana panja monga choncho.

²⁹⁰ Iye anati, “Iwo akuyikira msampha iwe. Iwo akakupempha iwe kuti ukalankhule pa Ministerial Association of Greater Chicago.” Anati, “Iwo akuyikira msampha iwe, pa kuphunzitsa kwako kwa Mawu Anga.”

²⁹¹ Iye anati, “Tsopano, iwo akasintha malo amenewo kumeneko. Iwo sakawatenga amenewo. Ndipo iwo akatenga ku malo, kumene ali a bulawuni.” Anati, “Apa iwo akuwoneka.” Ine ndinayima, ndipo ine ndinadziwona ndekha pa ngodya; ndinayang’ana mmbuyo umo ndipo ndinawona. Ine ndinawawona iwo onse kumeneko. Ine ndinawawona iwo onse azitumiki atakhala pamenepo, momwe iwo analiri. Ine ndinawayang’ana iwoponsepo. Ndipo Iye anati . . .

²⁹² “O,” ine ndinaganiza, “kuli bwino ine ndisapite kumeneko ndiye, Ambuye, ngati iwo ati akachite zimenezo. Ine sindikufuna kuwapweteketsa kumverera kwawo kapena kuchita chirichonse cholakwika.”

Iye anati, “Pita. Ine ndiyima pambali pako.” Iye anatero. Ndiko kulondola.

²⁹³ Tsopano, inu nonse, pali mboni pomwe pano, anali atakhala pamenepo ndipo akudziwa kuti izo nzowona. Uko nkulondola. Chabwino, inu muli nawo matepi kuno, naponso. Koma, ndi zimenezotu, inu mukuwona.

²⁹⁴ Tsopano, tsopano apa pali chinsinsi cha izi. Ndipo tsopano, Icho, pamene Icho chinawululidwa kwa ine molawirira mmawa uno, kuwala kwa tsiku kusanati. Ndiye ine ndinapita mwamsanga ku Lemba ndi kuyamba kuyang'ana, kuzifufuza izo. Apo izo zinali. Zitatu za izo, mpaka apa, zakhala mwamtheradi, zikuwululidwa mwauzimu. Eya. Tsopano apa pali chinsinsi cha kavalo wakuda, malingana ndi chimene chinawululidwira kwa ine.

²⁹⁵ Iye wayamba kumukwera iye mu nthawi ya mibadwo ya mdima. Ndicho chimene kavalo wakuda ankayimira, mibadwo yamdima, pakuti inali nthawi ya pakati pa usiku kwa okhulupirira owona amene anatsala. Yang'anani tsopano mu m'badwo wa mpingo umenewo, m'badwo wa mpingo wapakati uwo, m'badwo wa mpingo wamdima. Yang'anani momwe Iye akuti, "Iwe uli nazo mphamvu pang'ono zokha." Iwo unali pakati pa usiku kwa iwo, kwa okhulupirira owona. Tsopano yang'anani. Mwakuchitika chiyembekezo chonse chinali chitachotsedwa kwa Mpingo wooka, pakuti munthu uyu ankalamulira zonse mpingo ndi dziko. Kodi iwo akachita chiyani? Onani, Chikatolika chinali chitatenga malo, zonse mpingo ndi dziko. Ndipo onse, amene sanagwirizane nacho Chikatolika, ankaphedwa. Ndicho chifukwa chake iye anali pa kavalo wakuda. Ndipo yang'anani chinthu chakuda chimene iye anachita, onani, ndiye inu mukhoza kuwona. Ndipo inu basi. . . Ngati inu mukuyidziwa mbiriyakale yanu, iyang'anani iyo, ndiye inu mudza. . . Chabwino, inu simudzasowa ngakhale kuyidziwa iyo, kuti—kuti mudziwe Ichi. Tsopano yang'anani. Chiyembekezo chonse chinali chitapita. Ndiye kavalo wakuda wake.

Tsopano, iye anakwera pa kavalo woyera wake, chenjerero.

²⁹⁶ Ndiye iye anapatsidwa mphamvu; iye anatenga mtendere, anapha mamilioni. Ndicho chimene iye anakachita pamene iye anakawerabe mopyola. Ndipo iye akuchitabe icho. Mwawona?

²⁹⁷ Tsopano, apa iye ali pa kavalo wakuda wake tsopano, akutulukira. M'badwo wa mdima, iyo inali nthawi imeneyo. Chabe pafupi nthawi mpingo utatha kukhazikika, ndi atakhala mu mphamvu, iwo anafaniza china chirichonse. Ndi kupita kupyola, pafupi, mazana ndi mazana ndi mazana a chaka, ndi chimene muwerengi aliyense amadziwa ngati mibadwo ya mdima. Ndi angati amadziwa zimenezo? [Osonkhana ati, "Ameni."—Mkonzi.] Ndithudi, mibadwo ya mdima. Apo pali kavalo wakuda wanu, kuyimira m'badwo wa mdima uja. Tsopano, chiyembekezo chonse chitapita; popanda chiyembekezo konse. Chirichonse chinkawoneka chakuda, kwa okhulupirira aang'ono. Tsopano, ndicho chifukwa chake iwo ukutchedwa, kuyimiridwa, kavalo wakuda.

298 “Miyeso yake, kapena milingo yake, mu dzanja lake,” inu mukuwona. Kuyitanira uko, “Muyezo wa tirigu wogula rupiya, ndi miyezo itatu ya barele yogula rupiya.” Onani, makamaka, ameneyo ali, tirigu ndi barele ndi zakudya zathupi za moyo. Ndicho chimene buledi ndi chakudya chimapangidwa nazo. Koma, inu mukuwona, iye anali kulipiritsira izo. Chomwe icho chimatanthawuza, kuti, iye anali kulipiritsa omumvera ake kwa mtundu wa chiyembekezo cha moyo umene iye anali kutumiza kwa iwo, mwa kupanga. . .Iye anayamba mu nthawi yomweyo, ya kuwapanga iwo kulipirira mapemphero, kulipiritsira pemphero. Iwo akuchitabe zimenezo; manovena.

299 Chifukwa, anali kuchita chiyani iye? Kulanda chuma cha mdziko. Mulingo, kumayezetsa, “Muyezo wa tirigu wogula rupiya; miyezo itatu ya barele yogula rupiya.” Wokwera pa kavalo wakuda, mukuwona, iye anali kupanga. . .kuwalanda omumvera ake ndalama zawo. Pamene, Baibulo likuneneratu kuti iye akugwirizira, pafupi, chuma cha mdziko. Monga ife tinanena usiku watha za Russia, ndi zonse izo, iwo akutenga basi ndalama zonse ndi kungowalanda anthu chirichonse chimene iwo alinacho, chirichonse. Kotero, ndi zimenezotu.

300 Tsopano zindikirani. Inu mukuwona kumene kutenga kwakale kwa ndalama uko, mu mpingo, kukuchokera? Chokani kwa zinthu zimenezo; kuti mumange bungwe, chinachake chachikulu, miliyoni-dola apa. Ndipo—ndipo inu mukuwona amene ali manthu wa izo?

301 Zikomo Inu, Ambuye. O, mai! Ndine wokondwa kwambiri. Inde, bwana. Chabwino. Chakhala chiri chisomo Chake. Ndizo zonse. Chabwino. Chabwino.

302 Iyo inali nthawi ya pakati pa usiku. Kodi inu mukumvetsa zimenezo tsopano? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Ndipo apa iye akulipiritsira mtundu wa moyo, ndiye barele wake ndi zakudya, zachirengedwe; sizinali zauzimu, tsopano. Iye anali barele, onani, kotero, ndi mkate wa barele ndi mkate wa tirigu. Iye anali kulipiritsira moyo wa mtundu umenewo umene iye anali kuwupereka kwa omumvera ake. Kulipiritsira pemphero la wansembe, kuti awapempherere anthu achoke ku purigatorio. Kulipiritsa! Tsopano ine ndikutenga izi kuchokera mu mbiriyakale. Kulipiritsira, ine ndikuganiza, ndi novena, ine ndikuganiza, aliyense akudziwa chimene chiri. Novena, ine ndikuganiza ndicho chinachake iwe uyenera kuchichita, inu mukudziwa, kudizunza kwina. Winawake ayenera kulipiritsa zimenezo. Kubweretsa chuma cha mdziko kwa iye, kwa iyemwini, kulowa mu mpingo iwowokha. Ndipo iye akukwerabe. O, ndithudi iye ali. Inde, bwana. Akanakwerabe!.

303 Zindikirani. Apa pali gawo labwino tsopano. Zindikirani.

. . .ona kuti *iwe usawononge ayi* vinyo uyu ndi mafuta.

304 “Pang’onong’ono chabe a Iwo anatsalira kumeneko, koma usati iwe uwakhudze Iwo!”

305 Tsopano, mafuta ali...amaphiphiritsira Mzimu, Mzimu Woyera. Ine ndikupatsani inu ndime pang’ono ngati inu mukufuna kutero. Pali Malemba awiri. Mu Levitiko, 8:12, pamene Aroni, iye asanalowe mkati, ankayenera kudzozedwa ndi mafuta, inu mukudziwa. Ndipo mu Zakariya 4:12, za mafuta kubwera, akutsanuliridwa kupyola mmipope, ndipo anati, “Uwu ndi Mzimu Wanga, Mafuta.” Chinthu china, ngati inu mukufuna kuwona Mateyu, 14...25, apo panali mkwatibwi wopusa, kapena 25:3, namwali wopusa analibe Mafuta, analibe Mzimu. Ndipo Mateyu 25:4, namwali wochenjera anali nawo Mafuta mu nyali yake, wodzazidwa-Mzimu. Mzimu! Mafuta amayimira Mzimu. O, ulemerero! [M’bale Branham akuwombetsa manja ake pamodzi kamodzi—Mkonzi.] Chabwino. Inu mwamvetsa zimenezo? [Osonkhana ati, “Ameni.”] Chabwino. Tsopano, mafuta amayimira Mzimu.

306 Ndipo vinyo amaphiphiritsira kukondoweza kwa vumbulutso. O, ine—ine ngati kuti ndi thamange pa malo onse. Ndikudabwa ine sindinawadzutse oyandikana nawo, pamene Ambuye anandiwonetsa ine zimenezo, onani, “kukondoweza kwa vumbulutso.” Mwawona?

307 Mafuta ndi vinyo, mu Baibulo, zimagwirizana pamodzi, nthawizonse. Ine ndiri nayo milozo ndipo ndinayang’ana. Ulipo mndandanda wa iwo, kuyi monga—monga *choncho*, kumene vinyo ndi mafuta amapita limodzi, nthawi zonse. Mukuwona?

308 Pamene Chowonadi cha Mawu olonjezedwa a Mulungu chakhala chitawululidwa mowona kwa overa Ake amene adzazidwa nawo Mafuta, iwo onse amakondowedwa. Vinyo ali kukondoweza. Ulemerero! Ine ndikumverera iko pakali pano. Kukondowedwa nacho chisangalalo, kufuwula! Mwawona? Ndipo, pamene Iko kutero, Iko kumakhala nako kuchita komweko pa iwo kumene—kumene vinyo amachita pa munthu wachibadwa. Chifukwa, pamene vumbulutso laperekedwa, la Chowonadi cha Mulungu, ndipo wokhulupirira wowona atadzazidwa nawo Mafuta, ndipo vumbulutso liri lowululidwa, kukondoweza kumakhala kwakukulu kwambiri mwakuti Ilo limamupanga iye kuchita mosakhala mwachizolowezi. Kulondola. Ulemerero! [Osonkhana akusangalala—Mkonzi.] Onani, ndilo vuto ndi iwo tsopano. Ndiko kulondola, kukuwapangitsa iwo kuchita mosayenera.

309 Tsopano, ngati inu mukufuna Lemba la izi, ingoyambani kuweringa Machitidwe 2. Pamene iwo ali? Iwo anali nalo lonjezo lomwe linali litaperekedwa kwa iwo. Pamene lonjezo lonse la Mzimu Woyera linatsanuliridwa pa iwo. Ndipo zinali... Izo zinali zotsimikiziridwa Mwamalemba. Tsopano, inu mukuwona, a... .

310 Bwanji ngati iwo akanati... “Tsopano, dikirani, Iye anatiwuza ife kuti tiyembekezere pamwamba pano kwa utumiki wathu.” Ndipo atatha masiku asanu ndi atatu, iwo akanati, “Chabwino, ine ndikuwuzani inu, anyamata,” Marko anatero kwa Mateyu, “Ine—ine ndikukhulupirira ife tiri nawo kale Iwo, amzanga. Kodi inu simukuganiza choncho? Taonani, ife tiri nawo kale Iwo. Pamene ife tikuyembekezera pa utumiki wathu tsopano, ife tikungoyenera kupita kunja, kukalalikira. Iye anatiwuza ife kuti tibwere pamwamba apa ndi kuyembekezera, ndipo ili ndilo lachisanu ndi chitatu ife takhala tiri kuno.”

“Chabwino, tiyeni tiyembekezere lina limodzi.”

311 Masiku asanu ndi anayi abwera. Ndiye Marko akubwera pamenepo, kapena—kapena—kapena mwinamwake mmodzi wa ena onse a iwo, Yohane, anati, “Ine—ine—ine ndikukhulupirira ife sitikuyenera kuyembekezera molalikiranso. Ine ndikukhulupirira ife tiri nawo kale Iwo. Si choncho inu?”

312 Ndiye ine ndikhoza kumuwona Simoni, chifukwa iye anali nawo mafungulo, inu mukudziwa. “Tsopano yembekezani miniti, anyamata! Lemba liri nacho chinachake choti linene za izi. Iye sanatiwuze ife chabe masiku angati kuti tikayembekezere. Iye anati, ‘Inu mukhale kumeneko kufikira! Inu mukhale kumeneko kufikira uneneri wa Yoweli utabwera pokwaniritsika, kufikira uneneri wa Yesaya utatsimikiziridwa.’”

313 “Pakuti ndi milomo yachibwibwi ndipo ndi malirime ena Ine ndidzalankhula kwa anthu awa. Ndipo uku ndiko kutsitsimutsa.” Uyu ndiye vinyo amene watsanuliridwa. Vinyo ndi chiyani, mu Baibulo? Kutsitsimutsa. “Uku ndiko kutsitsimutsa kumene kumachokera mu Kukhalapo kwa Ambuye.” Mwawona? Izo—izo ziyenera kukhala Mwamalemba tsopano. Mwawona?

314 Kotero, inu mukuwona, vinyo amayimira kukondoweza kwa vumbulutso. Ndipo pamene Mzimu Woyera unagwa, ndipo iwo anawona Moto wa Mulungu ukugwera pa iwo, mai, umene unayamba kuwakondoweza iwo. Ndipo chinthu choyamba inu mukudziwa, iwo anakondowedwa kwambiri mpaka anthu makamaka anaganiza kuti iwo anali oledzera, koma iwo anali atakondowedwa ndi vumbulutso. Ndi Mulungu. . . Ndi ili apa! Vumbulutso lotsimikizidwa la Mulungu, linapangidwa kumveka kwa iwo, iwo anali okondwa nalo Ilo. Mulungu analonjeza izo. Apa izo zinawululidwa kwa iwo, ndi kutsimikiziridwa kwa iwo. Ameni! Apa panali munthu atayimirira pamenepo, akuti, “Ichi ndi Chija! Uwu ndi Iwo!” Ndipo apo icho chinali, kukhala chikutsimikiziridwa mwa chizindikiro chomwecho ife tiri nacho lero. Apo chiri—apo pali kukondoweza mwa

vumbulutso. Mwawona? Ndipo, tsopano, iwo kwenikweni anali nawo Iwo ndiye.

315 Ndicho chifukwa chake Petro anakhoza kufika uko, ndi kunena, “Bwanji, inu amuna aku Yudeya, ndi inu amene mumakhala mu Yerusalemu, mverani kwa ine. Inu nonse Madokotala Auzimu, mverani kwa zomwe nditi ndikuwuzeni inu, onani.”

316 O, nzodabwitsa chotani! Kuwululidwa! Kuwululidwa! Iwo amakhala okondowededwa kwambiri pamene iwo anachiwona icho chikutsimikiziridwa. Icho nthawizonse chimatero basi. Icho nthawizonse chimatero.

317 Pamene ine ndinawona kuti Mulungu analonjeza kuchita chinthu china chake mu tsiku ili, pamene Iye analonjeza kudzamatula Zisindikizo izi mu tsiku lino lotsiriza! Ndipo inu simukudziwa chisangalalo, ulemerero, pamene ine ndinamuwona Iye akuwulula izi, kuyima pamenepo ndi kuziwona izo zikuchitika! Ndi kudziwa kuti nditengera munthu aliyense, ku makani: Iye sananene konse chinthu chimodzi kwa ife koma chimene chinachitika njira yotero. Ndiyeno kuwona chisangalalo chimene chiri mu mtima mwanga, pamene ine ndikuwona lonjezo Lake la masiku awa otsiriza, monga Iye analonjeza kudzachita zimenezo. Ndipo apa ine ndikuziwona izo zikutsimikiziridwa ndi kupangidwa kulondola mwangwiro. Ine ndiri chabe...Inu mumandimva ine ndikunena, “Ine ndikumverera mwachipembedzo.” Ndilo liri vuto. Kukondoweza kuli koyipa kwambiri, ine—ine—ine chabe—chabe pafupi kupita kukuduladula, inu mukudziwa. Kukondoweza, kuchokera ku vumbulutso! Chabwino.

318 Iwo amakhala okondowededwa kwambiri, pa—vumbulutso, kuti iwo anazindikiritsidwa, chabwino, lonjezo. Tsopano, o, mai! Apo panafalikira chisangalalo cha kukondoweza, mpaka anthu anati, “Iwo aledzera naye vinyo watsopano,” pamene Mulungu anawulula lonjezo Lake kwa iwo. Ndipo Iye sanangowulula kokha ilo, koma Iye anatsimikizira ilo.

319 Ndicho chimene ine nthawizonse ndanena. Munthu akhoza kunena chirichonse, eya, iye akhoza kukakamizidwa chabe kuti anene chirichonse; koma pamene Mulungu abwera mozungulira ndi kuchitsimikizira icho!

320 Tsopano, Baibulo linati, “Ngati pali mmodzi pakati pa inu, yemwe amati ali wauzimu kapena mneneri, ngati iye anena zinthu izi ndipo izo nkusachitika, ndiye musati mupereke chidwi kwa iye. Musati mumuwope iye, konse. Musati mumuwope munthu ameneyo. Koma ngati iye anena icho ndipo icho nkudzachitika; ameneyo ndi Ine, inu mukuwona. Ine, ndiri mu icho. Icho chikutsimikizira chifukwa ndiri Ine.”

321 Ndipo, ndiye, mkazi wamng’ono uja waku Samaria. Pamene Lemba linanena kuti Mesiya uyu akanadzachita zinthu izi,

ndipo apa Iye anayima ndi kuchita izo chimodzimodzi basi zomwe Lemba linanena. Iye anati, “Iye ali uko. Bwera, zamuwoneni Mwamuna! Kodi sichiri icho chimodzimodzi chinthu chomwe Lemba linati chikanadzachitika?” Mwawona, iye anakondowedwa nalo vumbulutso. Kodi uko nkulondola? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Iye anakondowedwa nalo vumbulutso, pamene ilo linatsimikiziridwa. Mwawona? Uko nkulondola. Iye anadziwa kuti apo panali . . .

³²² “Ife tikudziwa kuti Mesiya akubwera, Yemwe akutchedwa Khristu. Ndipo pamene Iye abwera, Iye adzachita zinthu izi.” Iye anaziwona izo.

Ndipo Iye anati, “Ine ndine Iye.”

³²³ Ndiye kukondoweza kunayamba. Ndipo ulendo iye anapita, akufuwula, ndipo mpaka kupyola mu mzinda. Iye anasiya msuko wake wakale wa madzi, ndipo anapita kumusi uko, ndipo anati kwa anthu, “Bwerani, muwone!”

³²⁴ Tsopano, ngati inu mukanangodziwa miyambo ya Kummawa, ndiko kulakwa kuti iye achite izo. Inde, bwana. Mkazi wa mtundu umenewo, palibe aliyense akanamvera kwa iye. Ayi, bwana. Onani, iye anali nacho chilemba, ndipo pamene iye. . . Ngati iye akanapita mpaka mu msewu monga choncho, ndi kumachita monga choncho, anthu a mumsewu osalabadira za iye.

³²⁵ Koma, m’bale, iye anali nawo Mawu a Moyo pamenepo! Iye anali atakondowedwa. Inu mukanakhoza. . . Izo zinali ngati kuyesera kuzimitsa nyumba, pa moto, pa tsiku la mphepo. O, apo pali chinachake chikukupiza iyo! Iye anali—iye anali wokonzeka. Inde. Iwo sakanakhoza kuchizimitsa Icho. Uwo unali Moto wa Mulungu ukuyaka. Inde, bwana. Iye anati, “Ngati inu simukukhulupirira kuti ziri choncho, inu mungobwera cha kuno kumene msonkhano ukuchitikira. Ine ndidzakuwonetsani icho kwa inu.” Eya. Ndi chimenecho. Eya. Inde, bwana.

³²⁶ Ndipo kotero anthuwo anapita kumeneko. Ndipo Iye sanachite chimenecho nthawi yina imodzi. Koma iwo anadziwa chinachake chinali chitachitika kwa mkazi ameneyo. Iye anali anasinthidwa, kotero iwo anamkhulupirira Iye. Inde, bwana. Iwo anakhulupirira pa Iye.

³²⁷ Chifukwa, “Chikhulupiriro chimadza pakumva, kumva lonjezo la Mulungu, Mawu a Mulungu, ndi kuwayang’ana Iwo akupangidwa chenicheni.” Chifukwa, Iwo ndi mbewu. Ndipo pamene Iyo yabzalidwa, Iyo idzatenga Moyo. Iyo idzabereka basi chimene Iyo ikuchilankhula. Ngati iyo siyitero, ndiye iyo siyiri Mbewu ya Mulungu. Kapena, wobzalayo sanadziwe momwe angayibzalire Iyo; Iye sanatamidwe ndi Mulungu, kuti abzale Mbewu. Iye akhoza kukhala akubzala Izo pamwamba pa thanthwe kapena chinachake. Mwawona? Kotero inu—kotero inu

mukuwona, wofetsa amafetsa Mbewu, Mulungu amasamalira Iyo, ngati Iyo igwera mu malo oyenera, inu mukuwona. O, mai!

³²⁸ Ndiye Icho chikunena chiyani kwa wokwera uyu mu zakuda? “Usati iwe uwononge vinyo Wanga ndi Mafuta Anga! Usati iwe uzikhudze Izo, vinyo Wanga ndi Mafuta! Ine ndiri nazo pang’ono chabe za Izo pansi apo, koma alipobe pang’ono pokha mmenemo. Eya. Tsopano iwe ukhoza kumapitirira kupyola ndi kuyeza moyo wonse wantundu umenewo umene iwe ukuwutulutsa; izo ziri kwa iwe. Iwe udzalipira zimenezo pansi apo. Koma pamene iwe uti upeze vinyo uyo ndi Mafuta, iwe uzisiye Izo zokha!” O, mai! Ngati iwe ungakhoze, ngati iwe . . .

³²⁹ Mwa kulankhula kwina, monga chonchi, “Ngati iwe ugwira zina za Nkhosa Zanga zochepa, zomwe zadzazidwa nawo Mafuta Anga ndi vinyo, onani, vinyo ndi Mafuta a Mawu angwiro, onani, ndipo iwe ukuti ukwaphe iwo. Chifukwa, iwe, iwe ukachita izo. Ndicho chimene iwe ukuchita. Usati iwe uwakakamize iwo kuti anene ‘Timuwone Maria,’ aliyense kapena kuchita chirichonse monga icho, kapena zina za zikhulupiriro zako. Iwe uchoitse manja ako pa iwo. Iwo akudziwa kumene iwo akupita, pakuti iwo adzozedwa nawo Mafuta Anga. Ndipo pakukhala odzozedwa nawo Mafuta Anga, iwo ali naye vinyo wa chisangalalo, chifukwa iwo akudziwa Mawu Anga a lonjezo, ‘Ine ndidzawawukitsa iwo kachiwiri.’ Usati upweteke Izo! Usati upite kukayesa kuwasokoneza iwo. Chifukwa, khala chabe kutali kwa Izo. Ayi.” Zonse . . .

³³⁰ Iye akuwatsimikizira Mawu Ake ndi kuwabweretsa Iwo mkati. Iwo ankadziwa. Iwo ankadziwa kuti iwo akanadzawuka kachiwiri. O, momwe ine ndimakondera zimenezo! Psyi! Iwo adzawuka kachiwiri. Apa pakubwera kavalo wakuda, akukwera tsopano, mibadwo ya mdima.

³³¹ Apo panapita kavalo woyera; ife tinawona chimene iye anachita, mwangwiro. Apa pakubwera kavalo wofiira; ife tikuwona chimodzimidzi zomwe iye anachita. Apa pakubwera kavalo wakuda. Inu mukuwona, iye ali wokwera yemweyo nthawi zonse, chimene iye akuchita, mpaka mmusi kupyola mu mibadwo.

³³² Tsopano ife tikupeza kuti, iye ankayeza izo ndi kulipiritsa izo, chimodzimidzi: tirigu, zachirengedwe, moyo wachirengedwe. Ndizo zomwe iwo ankakhala moyo nazo.

³³³ Koma, kuphiphiritsira; Mzimu, Mafuta; ndi chisangalalo cha vinyo. “Moyo wauzimu uwo, usati uwupweteke Iwo. Uwusiye Uwo wokha!” Mwinamwake, “Roma, usati iwe ukhudze Izo! Izo ndi Zanga! Izo ziri za kwa Ine!”

³³⁴ Tsopano ine ndiri nacho chinthu china apa ine ndikufuna inu kuti mudziwe. Zindikirani, icho sichinali chimodzi cha Zamoyo chimene chinati, “Usati ukhudze Mafuta ndi vinyo.” Kodi inu munazindikira izo? Zamoyo zinai zinakhala zikulankhula,

koma . . . Yang'anani, ndiroleni ine ndiwerenge chabe kuchokera apa, pang'onong'ono chabe, onani, tsopano.

. . . muyezo, rupiya, wogula—wogula . . . tirigu wogula rupiya, ndi miyezo itatu ya barele yogula rupiya; ndipo ona kuti iwe usawononge vinyo ndi . . . mafuta.

335 Tsopano mverani apa.

Ndipo ine—ndipo ine ndinamva liwu mkati mwa zamoyo zinai . . .

336 Chinali chiyani Icho? Mwanawankhosa! Ameni! Izo sizinali Zamoyo zinai. Mwanawankhosa ananena izo. Chifukwa? Iye akukatenga Ake Omwe. Awo ali a Iye. Iye wawawombola iwo. Mwawona? Ameni! “Usati iwe ukhudze Mafuta awo!” Ayi, bwana. Osati Zamoyo zinai, koma Mwanawankhosa anali Mmodzi amene ananena izo. Ndipo, o, mai! Mwanawankhosa! Osati . . . Zamoyo zinai sizinalengeze izi. Mwanawankhosa ananena, Mwiniwake.

337 Pamene Zamoyo zinai zinati, “Bwera ndipo dzawone,” ndipo iwo anapita, ndipo iwo anakawona icho monga choncho.

338 Ndipo Iye anati, “Muyezo wa tirigu kugula rupiya, ndipo kwa muy- . . . ndi mochuluka chotero monga izi, ndipo barele wochuluka chotero.” Koma ndiye Mwanawankhosa anafuwula, pakati pawo pomwe, anati, “Koma usati uwononge vinyo ndi Mafuta!” A-nha. Ndiko kulondola. O, mai! Mvera kwa izo, “Usati iwe uwononge Izo, mnyamata, kapena iwe udzalipira izo tsiku lina.” O, mai!

Hafu pasiti naini.

339 Chabwino, mwa kupambana kwa kumvetsa kwanga, ndi mopambana momwe ine ndikudziwira, ndipo ndi zonse zimene ine ndimakhulupirira mu mtima mwanga, ndilo tanthawuzo lowona la Zisindikizo zitatu izo. Ine ndikufuna kuthokoza Mulungu chifukwa cha izo. Ndipo ine ndinena ichi, kuti, ndilo vumbulutso lomwe Iye anandipatsa ine. Iye anapereka ilo kwa ine, vumbulutso la Izo. Ndipo ine ndikukhulupirira kuti ife tikukhala mu masiku otsiriza.

340 Mawa usiku ife tidzatenga wokwera pa kavalo wotumbululuka uyo. Ndipo tsopano ine sindikudziwa. Ine sindiri kudziwa. Mulungu akudziwa izo nzowona. Ine sindikudziwa chinthu chimodzi cha icho. Ayi.

341 Ine ndinayang'ana pa phunziro langa lakale limene ine ndinali nalo zaka zapitazo. Ine ndinamuwona M'bale Graham Snelling kanthawi kapitako; iye ayenera kuti wapita panja. Koma, ine ndikukumbukira pamene ine ndinkalalikira kuno, kale. Ine ndinayang'ana umo kuti ndiwone zomwe ine ndinalankhula zaka zapitazo. Tsiku limodzi ine ndinali kupita kupyola mu Bukhu la Chivumbulutso, ine ndinatenga onse anai okwera pakavalo pa nthawi imodzi.

³⁴² Ine ndinati, “Kavalu woyera, umenewo unali mpingo woyambirira, mosakayika.” Ine ndinawerenga izo kuchokera m’bukhu la Adventisti. Ndipo ine ndinawerenga chinachake mmenemo. Ine ndinati, “Umenewo unali mpingo woyambirira umene unatulukira, ukugonjetsa.” Ndipo wotsatira anali kavalo wakuda, ine ndinati. . . ine ndayiwa tsopano chimene ine ndinachitcha kavalo wakudayo. Ine ndinati. . .

³⁴³ Kapena, “Kavalu wofiira,” kani, ine ndinati, “kavalu ameneyo mwinamwake akutanthawuza kuti—kuti vuto liri panjira, ndipo ilo litanthawuza nkondo zambiri zidzabwera, kapena chinachake monga icho.” Ine ndinati, “Mwinamwake padzakhala nkondo zambiri.” Ine ndinati, “Ndicho chimene icho chikanadzakhala.” Ndiyeno ine ndinati, “W—wotumbululuka kav- . . .”

³⁴⁴ Kapena, “K—kavalu wakuda,” ine ndinati, “uyo—uyo akutanthawuza kuti—kuti mwinamwake padzabwera nthawi yakuda pa dziko lapansi, pamene nyenyezi zonse zidza—zidzasiya kuwala; dzuwa lidzalowa, ndipo mwezi sudzapereka kuwala kwake.” Ine ndinati, “Ndicho mwinamwake icho chikutanthawuza.”

³⁴⁵ Ine ndinati, “Kavalu wotumbululuka, uyo akutanthawuza matenda ambiri akubwerapo.” Tsopano, ine sindikudziwa chomwe icho chikutanthawuza. Koma, ndicho, uko kunali kumasulira kwanga kwa icho ndiye, chifukwa ine ndinangochitenga icho mopambana mmene ine ndikanathera, nditayima apa mu guwa.

³⁴⁶ Koma, o, ine ndinali pafupi kunena chinachake! Chabwino. A! O! Inu mudza—inu mudzawona. Yang’anirani chabe, onani.

³⁴⁷ Tsopano, o, kodi ife sitiri okondwa chifukwa cha ora ili lomwe ife tikukhalamo! [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Pamene ife tiwona zinthu zonse izi zikulunjika mmwamba, ine ndikuganiza:

Mafuko akusweka, Israeli wadzuka,
Zizindikiro zimene aneneri ananenera;
Masiku a Amitundu akutha, ndi zovuta
zikuchuluka;
“Bwererani, omwazika, kwa inu eni.”

Tsiku la chiwombolo liri pafupi,
Mitima ya anthu ikulephera ndi mantha;
Dzazidwani nawo Mzimu, nyali zanu
zokonzedwa ndi zowala,
Yang’anani mmwamba, chiwombolo chanu
chiri pafupi! (O, mai!)

Aneneri abodza akunama, Chowonadi cha
Mulungu iwo akuchikana,
Kuti Yesu Khristu ali Mulungu wathu;

Kodi inu mukhulupirira Zimenezo? [Osonkhana ati, "Ameni."—Mkonzi.]

Koma ife tidzayenda kumene atumwi anaponda.

Pakuti tsiku la chiwombolo liri pafupi,
Mitima ya anthu ikulephera ndi mantha;
Dzazidwani nawo Mzimu, khalani nazo nyali
zanu zokonzedwa ndi zowala,
Yang'anani mmwamba, chiwombolo chanu
chiri pafupi!

³⁴⁸ Kodi sizodabwitsa zimenezo? [Osonkhana ati, "Ameni."—Mkonzi.] Ine ndimakonda zimenezo. Chiwombolo chiri pafupi.

Ndipo kudzakhala Kuwala mu nthawi ya madzulo,
Njira ya ku Ulemerero inu zedi mudzayipeza;
Mu njira ya madzi, kuli Kuwala lero;
Kumizidwa mu Dzina lopambana la Yesu.
Ana ndi akulu, lapani machimo anu onse,
Mzimu Woyera ndithu udzalowa mkati;
Kuwala kwa madzulo kwabwera,
Ndi chowona kuti Mulungu ndi Khristu ali Mmodzi.

Iye ali Mawu! O, mai! Zodabwitsa!

Posachedwa Mwanawankhosa adzatenga
Mkwatibwi Wake kukakhala nthawi zonse
pa mbali Yake,
Khamu lonse la Kumwamba lidzasonkhana;
O, adzakhala mawonekedwe aulemerero, onse
oyera mu zoyera zopanda banga;
Ndipo ndi Yesu iwo adzadya Kwamuyaya.

O, "Bwerani mudzadye," Ambuye akuyitana,
"Bwerani mudzadye;"

O, inu mukhoza kudzadya pa tebulo la Yesu nthawizonse;

Iye amene anadyetsa khamu, anasandutsa
madzi kukhala vinyo,
Kwa anjala akuyitana tsopano, "Bwerani
mudzadye."

O, "Bwerani mudzadye," Ambuye akuyitana,
"Bwerani mudzadye;" (Kudyerera pa
Mawu!)

Inu mukhoza kudzadya pa tebulo la Yesu nthawizonse;

Iye amene anadyetsa khamu, anasandutsa
 madzi kukhala vinyo,
 Kwa anjala akuyitana tsopano, “Bwerani
 mudzadye.”

³⁴⁹ O, mai! Kodi inu muli nayo njala? [Osonkhana akusangalala—Mkonzi.] “Odala ali iwo amene amva njala ndi ludzu la chilungamo.”

³⁵⁰ Kodi inu mukumkonda Iye? [Osonkhana anena, “Ameni.”—Mkonzi.] Kodi inu mukumkonda Iye? Fungulo kwa *Ine ndimkonda Iye*. inu mukudziwa. Tiyeni tonse tiyime chabe tsopano, ndi kukwezera mmwamba manja athu ndi kudzifotozoza tokha kwa Iye. “Ine ndimkonda Iye, ine ndimkonda Iye chifukwa Iye anayamba kundikonda ine.” Chabwino, tonse palimodzi tsopano.

Ndimkonda Iye, Ndimkonda Iye
 Poti Iye anayamba kundikonda
 Nagula chipulumutso changa
 Pa mtengo wa Kalvare.

³⁵¹ [M’bale alankhula mu lirime lina. M’bale Branham ayimikira—Mkonzi.] Mwaulemu kwenikweni basi. Ife tiri naye womasulira apa, M’bale Higginbotham. Ine sindikudziwa ngati iye ali pano usiku uno, kapena ayi. Ife tikufuna tipeze zomwe Iye wanena kwa ife. Dikirani chabe miniti imodzi. Apa, apa . . . [Mlongo apereka kumasulira.]

³⁵² Ndithudi, Ambuye alemekezeke! Chikhulupiriro changa chakwezedwera mmwamba mwa Mulungu. Inu, inu mukumkonda Iye, usiku uno, ndi mtima wanu wonse? [Osonkhana, “Ameni.”—Mkonzi.] O, mtamandeni Iye, ndi kunena, “Zikomo Inu, Ambuye Yesu!” [Osonkhana akutamanda Mulungu.]

³⁵³ Momwe ife tikukupatsirani Inu matamando, ndi mitima yathu yonse, Ambuye! Ulemerero kwa Mulungu!

³⁵⁴ Zingomupatsani Iye matamando, inu nonse anthu. Mulungu akhale ndi inu! [Osonkhana akupitiriza kusangalala ndi kutamanda Mulungu—Mkonzi.]



CHIVUMBULUTSO CHA ZISINDIKIZO ZISANU NDI ZIWIRI
(The Revelation Of The Seven Seals)

Mauthenga khumi awa analalikidwa ndi M'bale William Marrion Branham pa Marichi 17 mpaka pa Marichi 24, 1963, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., ndipo *Chisindikizo Chachisanu ndi chiwiri* chinapitirira pa Marichi 25 ku Sherwood Motelo. Titapeza matepi apachiyambi omveka ndi otsirizika kwathunthu, Mauthenga awa abwerezedwanso molingana ndi dongosolo latsopano. Kuyesesa konse kwapangidwa pochotsa molondola Uthenga wolankhulidwa pa matepi a maginito kupita ku tsamba losindikizidwa, ndipo atsindikizidwa mkatimu mosachotsera mawu ena.

Maufulu onse mu bukhu ili ndi osungidwa. Bukhu ili silingagulitsidwe, kapena kusindikizidwanso, kumasuliridwa mu zilankhulo zina, kapena kugwiritsidwa ntchito popezera ndalama wopanda kufotokoza kwa chilolezo cholembedwa cha William Branham Evangelistic Association. Kunasindikizidwa kachiwiri mu 2005.

CHICHEWA

©1994 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.

www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org